Lero Lemba Iri Lakwanirisidwa

Jeffersonville, Indiana, USA
Feburuware 19, 1965

1 Tangokhanichiimire chomwecho, ngati mungathe, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu kwa liwu lapemphero.

Okondedwa Atate a Kumwamba, ife tikukuyamikani usiku uno chifukwa cha ichi, mwayi winakuti titha kubwera ndikupereka uthenga uwu wa ulemerero, odabwitsidwa wa YesuKhristu. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa choti Iye adakali yemweyo dzulo,lero, ndi kunthawi zonse. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha anthu awa ameneasonkhana pano inu nthawi iyi yodzidzira, ndiposo ndi chiyembekezo chawo chopambana, kuyang'anira, ndikukhulupirira kuti china chake chosazoloweka chiperekedwa kwa ife kuchoka kwa Mulungu. Ife timabwera ndi chiyembekedzo chimenecho, Ambuye, ku msonkhano uliwonse. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha misonkhanoya usiku wa dzana, ku kachisi; Tikukuthokozani Inu chifukwa cha msonkhano panousiku watha, ndi chifukwa cha msonkhano wa lero, ku kachisi. Ife tikuyembekezera tsopano ku chomwe muli nacho kwa ife usiku uno.

Atate,ife tikudziwa kuti wina aliyense yemweali ndi kuthekera koyendetsa manja ake angakhoze kuvundukula masamba a Baibulo,koma pali M'modzi yekha Yemwe angalipange Ilo kukhala lamoyo ndi kukhala zenizeni,ndipo ameneyo ndi Inu. Ndipo, Atate, ife tikuyembekezera Inu kuti muchita ichousiku uno. Tidalitseni ife mu njira zonse. Mitima yathu ndi yodzala kwambirindi chimwemwe m'mene ife tikuona nthawi ikuyandikira pomwe ife tikupita kukakomana Naye, maso ndi maso, Iye amene ife tamukonda ndikumukhalira moyo kwazaka zonsezi. Otembenuka mtima atsopano ambiri, Ambuye, apangidwa. Pomvetsetsakuti gulu lalikulu, makumi anayi kapena asanu, akhala akubatizidwa mu DzinaLanu m'mawa, achokeso mu msonkhano wa usiku watha. O, Mulungu, chondepitirizani, ife tikupemphera, mpaka Mbewu yonse yokonzedweratu ya Mulungu itaona kuwala kwa Uthenga, ndipo yabwera mu khola.

Ife tikukupemphani Inu kuti mutibise ife usiku uno kuseri kwa Mawu; tipatseni ife khungu ku zinthu za dziko lapansi, ndipo tiloreni ife timuone Yesu. Mulore kuti pakhale zochitika za pa phiri lowalitsidwa pakati pathu, usiku uno, kuti ife tisaone munthu koma Yesu yekha. Ife tikupempha izi mu Dzina Lake, ndi kuulemerero Wake ndikutsimikiziridwa kwa Uthenga Wake. Amen. Inu mutha kukhala pansi.

2 Ine ndikungoti basi nditembenuze chimkuza mau ichi, kapena tebulo iyi, basipang'ono cha kumbaliku, ngati izo nzolondola, kotero kuti ine nditha kumaonambali zonse za osonkhana. Ine ndikuganiza kuti nditha kupeza zinkuza mawu izipozungulira pano molondora. Nkulondola, mwa kamphindi basi.

Ifetikupereka moni, kuchokera kuno ku malo olakhulirako enieni usiku uno, abweziathu ku Arozona, California, Texas, ndikudutsamu United States, mwa njira ya lamya.Ichi zikupita modutsa fuko lonse, msonkhano uwu usiku uno, mwa njira ya lamya.Ichi, ichi chikupita kufuko lonse, uthenga uwu usiku uno, mwa njira yalamya,ndiyeno ife tikudalira kuti Mulungu atidalitsa ife.

Mukukhoza kumva, kumbuyo uko kwa malo o-olankhulira awa chakumanzereku? Chabwino, iwoakupita kuti aone pano zochitika za lamya, kuti aona ngati izo ziri kungwiza bwinontchito.

3 Kodialiyense ndiwokondwa usiku uno? (Osonkhana anena, Ameni -Nkonzi) mukuti, izo ziribwino!Kumbali iyi? ("Ameni.") Ameni. Ine ndine okondwa kuona kuti inu nonse mwakhala momasuka.Ndipo tsopano mawa usiku, ngati gulu lipitirira kukula, iwonso adzakhala akumvapa lamya. Aliponso usiku uno. Ine ndikunganiza kuti ena mwa iwo ali kumunsi ukokukachisi. Ndipo, mawa m'mawa, misonkhano siizakhoza kukhala ku kachisi,chifukwa ku. . . kudzakhala osamala maluwa kumeneko akukongoletsa kachisichifukwa cha ukwati omwe uchitike mawa masana. Ndipo iwo asunthira mi - misonkhanoyo,m'mawa, ku tchalitchi cha M'bale Ruddell, m'modzi wa othandizana nafe, ndikumtunda uko ku msewu waukulu kuno, 62. Kodi izo zalengezedwa? (M'bale Neville anena, "Inde" - Mkodzi.) Izo zalengezedwa. Ndipo, ngati ukokungadzadzadze kwambiri, tidzatengapo otsalawo ndikutumiza mtumiki wina kumusiku tchalitchi cha M'bale Junior Jackson, uko ku Clarksville. Chifukwa chomwetikukhala nawo iwo kwa M'bale Rudell, ndi choti apa mpafupi, ndipo ife titha .. . Ndipo timaganiza kuti iza zikanakhalazophwekerapo kwa inu. Ndiyeno ife tidzasamala izo mwa njira ina. Ndipo mukhaleotsimikizira kuti mubwera ndi obatizidwa onse awo mawa, ndipo ndikuyembekezerakuti padzakhala ena zana kapena awiri owonjezera kwa obatizidwawo mawa.

Ndipo tsopanomawa usiku . . .

4 Inesindikonda kulengeza chirichonse chomwe iwe ungachilakhule nthawi isanafike,koma usiku wina mu msonkhano, kapena tsiku lina ine ndikufuna ndiyankhule paphunziro la: Kodi Melkizedeki Uyu ndi Ndani?Chifukwa, ili ndi - ndi phunziro limene ine ndikuganiza kuti ife tikukhala munthawi pamene mavumbulutso awa, omwe akhala ali funso kupyolera mu m'badwo,la, "Kodi munthu uyu ndi ndani?" Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Mulungu alinalo yankho, la chomwe Iye anali. Ena amati, "Unsembe," ena amati, "mfumu," ena . . . Koma payenera . . . Pokhapokhangati pali mfunso, apo payenera kukhala yankho ku mfunso limenero, lomwendililolondora. Sipangakhale mfunso popanda poyamba kukhalapo yankho

5 Tsopano,ine tikudalira kuti Mulungu atipatsa ife mdalitso usiku uno kuchokera mu Mawu Ake,momwe

ife tikuwerenga Iwo. Ndipo inu mwakhala . . . Billy anandiuza ine kutindikuuzeni inu kuti zedi inu mwakhala ndi mgwirizano wabwino ndi anthu kunoomwe akhala mu zochitika za momwe anthu angaimitsire magalimoto, a polisi ndi zinazonse. Pitirizani kutero; Izo ndi zabwino kwambiri.

Ifetikuyembekezera kuona nthawi, mwina mtsogolomu, pamene mwina tidzakhozakubweretsa hema kuno mu mzinda ndikuika iyo kunja kuno ku bwalo la mpira,kumene ife titha kukhala kwa nthawi yaitali, mwina kwa masabata atatu kapenaanayi, kukhala ndi chitsitsimutso, mowirikiza. Ndipo pano tikungoyetserakudziwana wina ndi mzake, ndiyeno apo nkusadzikana ndikumapitsanso kawiri. Komaine ndikanakondwa nditabwera kwa nthawi yotalikirapo, nthawi ina komwe tingakhaleopanda kutseka mu usiku kapena mausiku awiri, koma kungokhala ndikumaphunzitsa,usana ndi usiku, usana ndi usiku mosalekeza. Mwina wina akhoza kupita ku nyumbandikukadyetsa nkhuku, kukakama ng'ombe mkaka, ndikubweranso sabata yotsatirayondikumapitiriza ndi misonkhano. Ine - Ine ndimakonda zimenezo. Kotero Ambuyeakhale nanu.

6 Tsopano,ndisanachoke, mwina Lamulungu m'mamawa kapena Lamulungu usiku, kapena nthawi yina,imodzi mwa misonkhano iyi, ine ndikudziwa kuti nonse mukuyembekezera kumva Uthengapa Choonadi cha Chikwati Ndi Chilekaniro, chomwe liri limodzi mwa mavuto akulu atsiku ili. Ndipo ine nditsimikiza basi monga ndayama pano, Ine ndikukhulupirirakuti yankho lolondola liri M'Mawu a Mulungu, ndipo ine ndikukhulupirira kutiicho ndi chifukwa chomwe ine ndinalonjeza kuti nditi ndibwerere.

Ndipoine ndikuganiza, mwachiziwikire, momwe ine ndidziwira, Ine ndikufuna kutindikhale ndi msonkhano wina kuno ku Jeffesonville, pa Lamulungu la Isitara,ndipo ife tidza. . . pa msonkhano wakutuluka kwa dzuwa, ndipo kenako la Mulungu la Isitara. Kotero tidzalengedzaizo zisanafike ndikuyetsetsa kuti mwina tipeze malo olakhulirako, ngatinkotheka, kapena kwina kwake, kwa laMulungu, mwina Loweruka kapena la Mulungu likubwerari. Ndiyenera kudzabwerandikupita pa ndege chifukwa mpafupi ndi nthawi … Ine ndiyenera ndifufuze izo,poyamba, molingana ndi zochitika zomwe ine ndili nazo, ndipo mmodzi wa-wa-wazochitika zanga mu California. Ndipokenako mwamsangamsanga zitatha izo, ine ndikuyenera kupita kumunsi uko ku-kuAfrica. Kotero dziwani izi ndipo muzitipempherera ife.

7 Tsopano,usiku uno, ine ndikufuna ndiitanire tcheru chanu ku gawo la Mawu a Mulunguopezeka mu mutu 4 wa Luka woyera. Mutu 4 ndiponso ndime ya 16, ziyambira, pomweYesu akulankhula.

. . . Lero Lemba ililakwaniritsidwa m'makutu mwanu.

Tsopanoife tikufuna titenge, kuchokera pa Izo, chitsimikizo cha momwe mawu a Mulungualiri a mphamvu! Tsopano, ife tonse titha kulingalira za zimangozo, komazimatendera mphamvuzo kuti izi zigwire ntchito. Ife titha kulingalira zazimango za makina, a galimoto, komanso zimatengera mphamvuzo kuti zipangitsamatayalawo kuti ayambe kugwira ntchito ndikuyamba kuyenda.

Tsopano,Yesu anali atabwerera ku-ku Nazaleti komwe Iye anakulira. Kuwerenga motsika pa Lembaili apa, ife tikupeza kuti iwo anati, "Ife tinamva kuti inu munachita zakuti -ndi - zakuti uko mu Kapernao. Tsopano tiloreni kuti tikuoneni inu mukuchitazomwezo kuno ku dziko lanu lomwe."

Yesuanati, "Mu-Mneneri akhala opanda ulemu koma m'dziko la kwawo ndimo." Ndipo,komabe, uko ndi komwe iwe wakulira, ndi komwe anthu akukudziwa iwe Ndipokumeneko Iye anali ndi-ndi-ndi dzina loipa, poyamba pomwe, pokhala Iye obadwaopanda atate wa pa dziko lapansi. Iwo anamutcha Iye "Mwana wa pathengo," kutiMaria makamaka anakhala oyembekezera iye asanakwatitsidwe, movomerezeka, ndiYosefe. Koma, izo sichoncho ai, ife tikudziwa kuti siziri choncho.

8 Ndipopa Lemba ili, chomwe chimandipangitsa ine kuti ndiike maso anga pa ili, ndichina chake chomwe changochitika posachedwapa mu Phoenix, Arizona. Ili linalitsiku lotsilidza la msonkhano lomwe ine ndinali oti ndiyakhule ku msonkhano wamkuluwa maiko wa Full Gospel Bussiness Men.Ndipo mu msonkhano wamkulu uwu munali mulendo pamodzi ndi ife, yemwe analibishopo wa Katolika, yemwe ali -ali wa "the ChadeanRites wa Apostolic Katolika Church;M'busa wamkulu John S.Stanley, O.S.D." Iye ndi " bishopu wamkulu wa mizinda ya muUnited States," mu mpingo wa Katolika. Izi ndizomwe zinali pa kadi yake ndi - ndikeyala yake.

Ndipoiye anali mlendo kwa a ChristianBussiness Men, ndipo ine ndinali nditamuona iye kumeneko, dzulo lake. Ndipopamenepo ine ndinali kulakhula utsiku wa Loweruka, ndikukhulupirira izo zinali,kapena Loweruka m'mamawa pa chakudya cha m'mawa, ndipo ine …. pamene inendinali kulakhula, iye ankangondiyang'anitsitsa ine. Ine ndimaganiza "munthuuyo wakhala apoyo sakugwirizana ndi zonse zomwe ine ndikunena." Ndipo, inumukudziwa, inu mukana - inu mukanakhioza basi kumuona iye; Iye amakhozakumangogwededza mutu wake pansi ndi pamwamba, koma ine sindinadziwe chomwekwenikweni chimamuchitikira iye.

9 Ndiyenola Mulungu masana, pamene ine ndinaimirira kuti ndiyakhule, ine ndinali kutengaphunziro langa pa za Ululu Wobereka, pomwe Yesu anati kuti, "Monga mzimayi alimuululu wobwereka mwana, "Iye akumva ululu wa kubereka. Ndiyeno ine ndinalindikufuna kuti ndiyankhule kuchokera apo, ngati, ululu wa

kubereka, phunziro,kunena kuti dziko liri mu ululu wa kubereka tsopano. Chakale chiyenera kutichithe, kuti chatsopano chibadwe; basi monga mbe - mbewu iyenera kuti iwola,kuti ipereka moyo watsopano. Ndipo pomwe ululu, ululu obereka wakantha dziko!Munkhondo yoyamba ya dziko lonse, ili linali ndi ululu woopsa, chifukwa analindi mpweya wa poison, ndi zina zotero, umene pafupipafupi ukanaononga dziko.Ndipo mu nkhondo yachiwiri ya dziko lonse, ilo linakathidwa ndi wina,ululuwolimbilako; Iwo anali ndi zophulitsa zazikulu, ndiponso ndi mabomba a atomiki.Ilo silingalimbe ndi ululu wina wobereka. Ndi ma mabomba awa amumlengalenga ndizinthu zina zalero, nkhondo ina imodzi ingaliponyere ilo kunja mmulengalenga,pakuti tsopano ilo liyenera kuomboledwa. Ndipo pamenepo padzakhala dzikolatsopano. Baibulo linati padzakhala.

Pansipa uthenga uliwonse wa mneneri, a Isirayeri amamva ululu wakubereka, chifukwakuti ananeri awa amabwerapo pa chochitikacho pamene a maphunziro a za umulunguawa ndi akuluakulu ampingo awa atabweretsa mpingo m'maonekedwe a bungwe. Ndipopamene aneneri awo amabwerapo pachochitikacho ndi PAKUTI ATERO AMBUYE,amagwedeza mipingoyo, ndi ilo limakhala ndi ululu wakubereka. Potsiriza, ilolinali ndi ululu wobereka mopitiriza mpaka linadzabereka mwana wa mwamuna wa Uthengawabwino, amene anali Mawu Iwo eni atasandulika thupi.

10 Koterompingo theradi ili mu ululu wobereka usiku uno, kamodzinso kuti libereke Mwana,Mwana wa Mulungu kuti abwerenso kawiri. Onse a zamaphunziro a zaumulungu athuawa, machitidwe athu onse, zipembedzo zathu zonse, zaoleratu paliponse pansipathu. Kotero ife tili mu ululu wobereka, ndipo Uthenga ochokera kwa Mulungunthawi zonse umaika Mpingo muululu waukulu, koma patapita nthawi ilo liberekaMkwatibwi. Izo zibweretsapo Yesu Khristu kwa Mkwatibwi Wake.

Ndipo,pamenepo, polingalira kuti munthu uyu wakhala asakugwirizana nane mochuluka.Pamene ine ndinayimirira kuti ndilankhule Uthenga uwu, Ine ndinatembenuzira muBaibulo langa kuti ndipeze tsamba. Ndipo mkazi wanga anali atangondipatsa ineBaibulo latsopano ngati mphatso ya Khristmasi. Baibulo langa lakale ndilapafupifupi zaka khumi ndi zisanu, ndipo Ilo linali litang'ambika mtidziduswa. Masambawo nthawi zonselikatseguka amaulukamo mwa ilo. Ndipo, koma ine ndinkadziwa komwe ndingapezeMalemba, kotero ine ndinawerenga kwambiri mu Baibulo ilo. Ndipo ine ndinangotenga chabe latsopanolo, chifukwalinalo linkaoneka mwakutha kwambiri, kuti ndipite nalo ku Tchalitchi.

11 Ndipopamene Ine ndinayamba kuvundukula mu Yohane Oyera, komwe Lemba linapezeka, inendinayamba kuwerenga mutu wa 16, ndipo ndime yomwe ine ndinali kuifuna apopanalibe. Kotero ine ndinaganiza, "Zachilendo!" Ine ndinavundukulanso Ilokachiwiri; komabe apo panalibe ilo. Ndipo M'bale Jack Moore, ochokera kuShreveport Louisiana, bwenzi langa wapamtima, anali atakhala pamenepo. Ine ndinati,"M'bale Jack, kodi ilo silimapezeka mu Yohane Oyera mutu wa 16?

Iye anati,"Inde."

Ndipowamsembe wa chikatolika uyu anaimilira pa mpando wake, kuchokera pakati pa azitumuki pafupifupi zanaomwe anakhala ku guwa; anayenda kufika pafupi nane, atavala zonse za minjiro yake ndi mikanjo ndi mitanda, ndi zina zotero, nafika pafupi nane. Ndipo iyeanati, "Mwana wanga, khazikika. Mulunguakukonzekera kuti ayende."

Ine ndinaganiza , "Bishop wa chikatolika kundiuza ine zimenezo?"

Iye anati,"Werenga izo kuchokera mu Bukhu langa."

Ndipoine ndinawerenga Lemba kuchokera mu Bukhu lake, ndipo ndinatenga phunziro langandikupitirira, ndikulalikira uthenga wanga.

Zitathaapo, pamene ine ndinatsiriza, iye anaimirira ine nditapita, ndipo anati, "Palichinthu chimodzi chomwe chitichichitike. Patatha izo, mpingo uyenera kutuluka munyansi zomwe iwo ulimo,kapena tiyenera kutuluka munyasi zomwe mpingo ulimo." Kotero chimodzi kapenachimkaze.

12 Ndipoine ndinali pa msewu ndikupita kwathu, ndikubwerera ku Tucson, usiku umenewo.Ana anali kulirira sagweji pa malo ang'ono ogulitsira. Ndipo mkazi wanga anati, "Bill, ine sindinakhalepo wamanjenjemoyo wanga onse, kukuona iwe utaima pamwamba paja ukuzungulira kupyola muBaibulo lija." Anati, "Kodi izo sizinakupange iwe kunjenjemera?"

Inendinati, "Ainso." Ine ndinati, "Ine ndinkadziwa kuti ilo linali momwemopenapake. Iwo basi analibe tsambalo m'menemo. Izo zinali zoti anaziphonyapotayipa."

Ndipoiye anati, "Kuganiza, kuti ine ndiyemwe ndinakupatsa Baibulo limene lija! Zimaoneka ngati disolirilonse m'mene munja limayang'ana pa ine."

Ndipoine ndinati, "Chabwino, iwe sukanathandizapo pa icho. Paja panali posalembedwa M'baibulo."Ine ndinati, "Kungoti iwowo sanaikemo tsambalo."

Chabwino,ine ndinalitenga ilo ndikuliyang'ananso kachiwiri basi mwangwiro momwezikanakhalira; koma

mutu wa 16 umathera, gawo, gawo lakelo basi pafupifupimainchesi atatu kuchokera pansi, mpaka pa mutu wa 17 ku mbali inayo, zimapanga chinthu chomwecho. Ndipo,pokhala Baibulo latsopano, masamba awiri amenewo anali atamatana mwangwiro,ndipo ine ndinali kuwerenga kuchokera pa mutu wa 17 mmalo mwa mutu wa 16.

"Chabwino," Ine ndinati,"Izo zonse zili bwino. Izo zinali pa cholinga chinachake."

13 Ndipobasi momveka bwino monga inu mukanamveraliwu lirilonse, Liwu linadza kwa ine, ndikuti, "Iye analowa mu Nazareti, komweIye analeredwerako; ndipo analowa mu sunagoge, monga chinaliri chizolowezi chake. Ndipo wamsembe anampatsaIye Malemba kuti awerenge, ndipo anawerenga Yesaya 61. Ndipo pamene iyenawerenga Malembawo, anakhala pansi; Anapereka kwa wamsembe Baibulo, Bukhulo,nakhala pansi. Ndipo maso a osokhana onse anali pa Iye. Mawu amtengo wa patali anatuluka pa kamwa lake. NdipoIye anati, 'Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.'"

"Lero Lemba ili lakwaniritsidwa." Ndimolondola bwanji momwe Malemba aliri! Ngati inu mungazindikire ichi muYesaya61:1-2 ndipomwe Ambuye wathuamawerengapo, Yesaya 61:1-2. Koma pakati pa ndime yachiwiri ya Yesaya 61, Iyeanaima. Pamene ilo linati, "Mzimu wa Ambuye uli pa Ine; kuti ndikalalikire chakachosankhika." Pamenepo Iye anaimachifukwa chiyani? Gawo linalo, kubweretsa chiweruzo, sizimagwirizana ndi KubweraKwake koyamba, koma Kubwera Kwake kwachiwiri. Mwaona, sizimagwira ntchito apo.Momwe Malemba salakwitsa! Iwo nthawi zonse amakhala angwiro. Yesu analekezabasi pomwe Lemba limathera, chifukwa icho chinali ndendende chomwe chinayenerakuonetseredwa mu tsiku Lake.

Tsopano, mu Kubwerakuja koyamba. Kubwera kwachiwiri Iye adzabweretsa chiweruzo pa dziko lapansi; komaosati pa nthawi imeneyo. Iye anali "oti alalikire chaka chosankhika."

14 ZindikiraniMesiya ataima pa guwa, kuti azizindikiritse yekha ndi Mawu a lonjezo a M'badwo umenewo.Nzodabwitsa motani, Mesiya akuimirira patsogolo pa mpingo! Ndipo anapenya pa Mawu awa a mtengo wapatali pamene akunenaapa, "Kulalikira chaka chosankhika."

"Chaka chosankhika," monga ife tonse tidziwa,monga owerenga a Baibulo, chinali "chakacha mamasulidwe." Kuti, pamene akapolo onse ndi andende onse, pamene iwo anali, kutengedwa, undende; ndipo amayesakupereka mwana wa mwamuna, kuti alipire ngongole; kapena mwana wa mkazi, kutialipire ngongole, [Malo opanda mawu patepi-Mkonzi.] ndipo iwo anali mu msinga.Zinalibe kanthu kuti iwo akhala nthawi yaitali bwanji mu msinga, kapena kutiiwo anayenera kuti akhale nthawi yaitali bwanji m'menemo; pamene chakachochibwera, cha mamasukidwe, pamene lipenga lalira, munthu wina aliyense amakhalaomasulidwa ngati amafuna kumasulidwa. [Malo opanda mawu pa tepi-Mkonzi.] Iwe wamasulidwa. Iwe sumakhalanso kapolo.

Komangati umafuna kuti ukhalabe kapolo, ndiyeno umayenera kutengedwa kupita kukachisi ndikuima pa nsanamira ya kachisiyo, ndipo amatenga chiotcherero ndipoamaboola bowo mu khutu lako, ndiye pamenepo umakhala kapolo kwa mbuye wakoyomoyo wako onse.

15 Ndi chitsanzo changwiro bwanji chomwe icho chili cha Uthengawa Yesu Khristu! Pamene Iwo ulalikidwa, mu nthawi yosankhikha, ndi nthawi yamamasuludwe; Wina aliyense, kaya ndiwe ndani, kaya ndiwe wa mtundu wanji, kayandiwe wa chipembedzo chanji, Kaya iwe wazama bwanji mu tchimo, kapena kuti vutolako ndi chiyani; iwe utha kukhala mfulu pamene wamva Lipenga la Uthengalikuomba. Iwe ndiwe mfulu! Koma ngati iwe mufulatira Uthenga naukana kuumvaiwo, zindikira, iwe umabooledwa mukhutu ndi chiotcherero. Izo zikutanthauzakuti, kunena, kuti iwe wadutsa mzere wapakati pa chisomo ndi chiweruzo, ndipo iwesudzamvanso Uthengawo kachiwiri. Iwe sudzapitirira aponso. Iwe uyenera kukhalakapolo kuzochitika zomwe iwe ulimo, masiku onse a moyo wako, ngati iwe ungakanekumva chaka chosankhika.

Tsopano,gawo lina la izo , monga ndanena, sizinafunike kuti ziyankhidwe, chifukwaMesiya uyu yemwe akubwera, mu kanthawi tsopano, ndi pomwe Iye ati abweretsechiweruzo.

16 Tsopano,ankalephera bwanji anthu awo kuona Yemwe Iye anali? Iwo anaziphonya bwanji izo?Izo zikanakhala bwanji, pamene izo zinalizitadziwitsidwa ndikuonetseredwa pambalambanda? Iwo akanati aphonye bwanjikuziona? Pamene Iye . . . Ndi Mawu otani? Tangolingalirani izo, "Lero Lemba ililakwaniritsidwa pa maso panu."

Ndani ananenaicho? Mulungu mwini Yekha, Yemwe ali otanthauzira wa Mawu Ake omwe. "Lero Lembaili lakwaniritsidwa." Mesiya, Mwiniwake, akuima pamaso pa osonkhanandikumawerenga Mawu kuchokera mu Baibulo, zokhuza Iye mwini, ndipondikumati, "Lero Lemba ililakwaniritsidwa," komabe iwo nkumalephera kuchiona Icho.

Ndizoopsa bwanji izo zingakhale, koma izo zachitika. Izo zachitika nthawi zambiri.Izo zingachite bwanji? Indedi, monga izo zinachitika mu nthawi zina,pokhulupirira kutanthauzira kwa Mawu kwa munthu. Izo ndizo zomwe zinapangitsa icho.Okhulupirira awo mu masiku aja, otchedwa-okhulupirira, amatenga

kutanthauzira komweansembe anali atanena za Malemba. Choncho Yesu, poti sankakhala nawo m'maguluawo kapena m'mabungwe awo, Iye anachotsedwa mu mgwirizano wawo. Ndipo, choncho,iwo sanamuzindikira Iye pakati pawo, chifukwa Iye anali osiyana nawo. Umunthuwa Yesu Khristu unali osiyana kwambiri kotero kuti palibe munthu akanakhozakuphonya kuona kuti uyo anali Mwana wa Mulungu, chifukwa Iye analikuonetseredwa kwa ngwiro kwa Malemba omwe analembedwa za Iye. Umo ndi momwe MKhristualiyese amadziwidwira, pamene moyo wake umazindikiritsa zinthu zomwezo zomwe MKhristuayenera kuchita.

17 MomweIye akanakhoza kuima pamenepo ndi kumati, "Lero Lemba ili lakwaniritsidwa pa maso panu!" Ndizapadera bwanji, ndi zapambalambandabwanji, komabe anthu aja sanazimvetse izo. Chifukwa chiyani? Ndi chifukwa iwoanatenga kutanthauzira kwa dongosolo lina la ansembe lomwe iwo amalimvetsera. Ndipombiri nthawi zonse imadzibwereza yokha. Ndipo Lemba liri ndi tanthauzo lapawiri pa ilo, ndi vumbulutso lapawiri.

Mwachitsanzo,monga limati mu Baibulo, kuti, "Kuchokera ku Aigupto Ine ndinayitana Mwana Wanga," kukamba za Yesu.Pezani umboni wa izo, ndipo mupeza kuti, izo zimakambanso za Yakobo, Lembalomwelo. Yesu anali Mwana Wake wamkulu. Yakobo anali mwana wake yemweanamuyitana kuchokera ku Aigupto, zomwe mu zowerenga za Scofield ndi zowerengazina zonse zimapereka kwa izo, chifukwa ilo linali Lemba lomwe linachitiraumboni ku icho. Kotero ilo linali ndi-ndi yankho lapawiri; ilo linali ndiyankho kwa Yakobo anaitanidwa kutuluka, komanso kwa Yesu kuitanidwa kutuluka.

Ndiponsoziri chomwecho lero! Ndi chifukwa kuti ife tiri mu chisokonezo chonga ichichomwe tirimo, ndipo anthu akulepherakuona Choonadi cha Mulungu, ndi chifukwa choti pali kutanthauzira kochulukakwambiri kwa Mawu a Mulungu kopangidwa ndi anthu. Mulungu safuna aliyense kutiatanthauzire Mawu Ake. Iye ndi odzitanthauzira Iye yekha.

18 Mulunguanati, Pachiyambi, "kuwale,"ndipo kunawala. Izo sizisowa kutanthauzirakulikonse.

Iye anati, "Namwaliadzaima," ndipo iye anatero. Izo sizisowa kutanthauzira kulikonse.

Pamene… kutanthauzira kwa Mulungu kwa Mawu Ake, ndi pamene Iye aonetsera ndikutsimikizira iwo kukhala chomwecho. Uko ndiye kutanthauzira kwake,pozipangitsa izo kuchitika. Apo pomwe pali kutanthauzira kwa Mulungu, ndi pomweamawapangitsa Mawu Ake kuchitika. Iye akuwatanthauzira Iwo kwa inu.

Mongangati kunakakhala kuti kunali kusanakhalepo kuwala, ndipo Iye anati, "Kuwale,"ndipo panali, izo sizisowa wina aliyense kuti atanthauzire. Koma ife timatengamachitidwe opangidwa ndi anthu ndikusakaniza mu Iwo, ndipo mukachita izo, inu -inu mumazichotsa izo mu mzere. Izo zakhala ziri chomwecho nthawi zonse.

19 Komaine ndidakaganizabe za kukhuza kwake momwe kumayenera kukhalira. Tangoganizaniza izo, Mesiyayo! Chifukwa chiyani iwo analephera kumuona Iye? Chifukwa, atsogoleri awo omwe, omwe anali otiakanamudziwa Iye, omwe anayenera kukhala okhazikika M'Malemba, omwe akanakhalaomvetsa Malemba, iwo anamuchepsa Munthu uyu ndipo anati, "Iye anali mwana wachigololo, poyamba pomwe. Ife sitingakhoze kukhulupirira Izo." Patapita zaka,ife sitimakhulupirira izi. Ife tingakhoze kufa pa cholinga chonena kuti Iyeanali Mwana obadwa mwa namwali. Ndipo kudzachitika tsiku lina kuti, zinthuzomwezi zomwe ife tikuona Yehova akuchita lero, amuna mu mibadwo ikudzayo,ngati iriko, adzafera chinthu ichi chomwe ife tikulankhula za icho lero. Inumuyesa kudzachita icho pamene chilemba cha chilombo chitabwerapo, ndipo iwe suloredwa kulalikira Uthengawumunjira iyi.

Pamene mgwirizanowaukulu wa mipingo ubwera pamodzi, omwe uli mu dongosolo pakali pano la mpingo wadziko,inu mudzayenera kusindikiza umboni wanu ndi moyo wanu omwe, ku Ichi.

20 Inumuyenera kukhulupirira Iwo lero. Ngati ansembe aja akanangodzuka, aja anamutsutsaIye, sakanakhoza kumutsutsa Iye.

"Koma," inumukuti, "ngati ine ndikanakhala kuti ndinali kumeneko, ine ndikanachitazakuti-zakuti."

Chabwino, uja sunalim'badwo wanu. Koma, uno ndi m'badwo wanu, ino ndiye nthawi.

Inumukuti, "Chabwino, ngati Iye akanakhala pano!"

Baibulolimati, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi ku nthawi zonse," yemweyo, kotero Iyeali pano. Koma, Iye ali pano. Monga kuti dziko latuluka, lakhala lopambana, ndilophunzira kwambiri; Iye ali pano mu maonekedwe a Mzimu, umene sangauphe kapenakuuika mu imfa. Iye anafa kamodzi; Iye sangafeso kawiri. Iye anayenerakupangidwa thupi ndi cholinga choti Mulungu akaphedwe mu thupi, kwa tchimo.Koma nthawi iyi sangakhoze kufa; Iwo ndi Mzimu Woyera.

21 Tsopano,kukalingalira kuti iwo anali nazo zinthu izo motsutsana naye! Chinthu china,kuti Iye sakanakhoza kulumikizana nawo mmagulu awo. Ndiyeno, mukuona izo komabezinamupangitsa Iye kukhala

munthu woipa. Iye sakanajowina ma-mabungwe awo,sakanajowina unsembe wawo, ndipo sakanakhala ndi chirichonse chochita ndi icho.Ndiponso, pambali pa zonsezo, Iye anayetsetsa kung'amba zomwe iwo anamangapo.

Iyeanalowa mu kachisi. Ife timamutcha Iye mamuna ofatsa; Iye anali, koma nthawizambiri ife sitimamvetsa kuti kufatsa ndi chiyani. Iye anali munthu wachifundo,komabe ife timalephera nthawi zina kumvetsa kuti kodi chifundo ndi chiyani.Osati chisoni cha umunthu, icho si chifundo. Koma, chifundo, ndi, "kuchitachifuniro cha Mulungu." Iye anadutsa pa thamanda la - la Betisida, chipatacho.Kumeneko kunagona anthu makamu a iwo. Makamu ndi nambala yosatsimikiziridwa.Koma uko kunagona makamu; opunduka, akhungu, osayenda, onyala. Ndipo Iyeanakhuzika ndi anthuwo, nthawi zonse. Ndipo Iye anapita kwa munthu m'modziyemwe sanali opunduka, wakhungu, osayenda, kapena onyala; mwina anali ndi vutola chikhodzozo, kapena iye anali ndi vuto laling'ono lomwe linakhazikika. Iyeanali nalo kwa zaka makumi atatu ndi zisanu ndi zitatu. Izo sizinali zoti zikanavutaiye, sizinali zoti zikanamupha iye. Iye anagona pa mphasa.

Ndipo Iye anati,"Kodi iwe ukufuna utachira?"

Ndipo munthuyoanati, "ine ndilibe aliyense oti andigwetsere ine m'madzi, koma pamene inendikubwera, chabwino, munthu wina amagwerano patsogolo panga."

Mwaona, iyeamatha kuyenda, amatha kuona, amakhoza kumayenda pozungulira, koma anangokhalaofooka.

NdipoYesu anati kwa iye, "Dzuka. Tenga kama yako nupite ku nyumba yako." Ndipo Yesuanafunsidwa mafunso pa icho, pakuti inu mukukumbukira kuti Malemba ananena izi.

22 Ndizosadabwitsa! Ngati Iye akanabwera ku Jeffersonille usiku uno nachita zinthungati zimene zija, akanazalankhulanso za Iye. Koma, kumbukirani, Iye anabwerakudzachita chinthu chimodzi icho chinali chifuniro cha Mulungu. Tsopano, izo zimapezekamu Yohane Woyera 5:19, inu mudzapeza yankho. Iye anati "Indetu, indetu, inendinena kwa inu, Mwanayo sangachite kanthu mwa Iye yekha; koma chomwe Iye aonaAtate akuchita, chomwecho Mwanayo amachita.

Tsopano,iwo anayenera kudziwa kuti icho chinali chitsimikizo cha uneneri wa Mosecho, "Pakuti Ambuye Mulungu Wanu adzakudzutsiraniinu mneneri onga ngati ine."

Kodiinu mundazindikira, pamene Iye anamuona munthuyo, Iye anati . . . Yesu anadziwakuti iye anakhala mu chikhalidwe chimenechi kwa zaka zambiri. Mwaona, pokhalamneneri, Iye anaona munthuyo mu chikhalidwe chimenecho; ndipo anapita kumunsiko nayenda modutsa-modutsa chozungulira anthuwo,mopaza pakati gulu, mpaka anampezamunthuyo. Anadutsa pa opunduka, osayenda, akhungu ndi onyala komabe ali munthuodzadza ndi chifundo. Koma, chifundo, ndi, "Kuchita chifuniro cha Mulungu."

23 Tsopano,ife tikumupeza Iye monga Iye sakana jowinana ndi iwo, sakanakhala ndi chochitamu magulu awo, kotero Iye anali otaidwa kunja. Iye sakanakhala ndi ... Pambali pa izo, Iye anapita mu kachisi tsikulina. Munthuyu analowa m'menemo ndipo anapeza nyumba ya Mulungu ili pafupiyoola monga iriri lero. Iwo anagula, kugulitsa, kumasintha ndalama. Ndipo Iyeanagubuduza matebulo a ndalamawo; natenga dzingwe naziluka, nawamenya osinthandalamawo kuwatulutsa kunja kwa kachisi. Ndipo anawayang'ana iwo ndi mkwiyo,ndipo anati "Kwalembedwa," Alleluya,"Nyumba ya Atate wanga ndi nyumba yopembedzeramo; ndipo inu mwaipanga iyokukhala mphanga ya mbala. Ndipo inu, ndi miyambo yanu, mwapangitsa malamulo aMulungu kukhala opanda mphamvu.

O,Kodi kagulu ngati kameneko kakanakhala komukhulupirira Iye? Ai, bwana. Iwoanali atazama mwaunkhumba mu zithaphwi za mabungwe ndi nyasi za tsiku limenero,kufikira anali ataumitsidwa kwambiri mwa kudzidziwa kwa uchipembezo mpaka kuti iwo sakanatha kumverera kugwedeza kwaMphamvu ya Mulungu wa Mphamvu zonse. Ndizosadabwitsa mkazi wam'ng'ono uja akanakhoza kukhudza chovala chake ndiponachiritsidwa mwa Icho; Ndipo mtsilikalioledzera akanatha kumulavulira Iye ku maso ndipo osamverera ukoma! Zimatengeramafikidwe ako pa Iwo. Zimatengera pa chomwe iwe ukufuna. Pamene iwe upita kutchalitchi, zimatengera pa chomwe iwe ukuyembekezera.

24 Tsopanoife tikumuona Iye ataima pamenepa. Mosadabwitsa koma chomwe anthu analiatamuchenjeza iye kale atamuchenjeza … ansembe anali atachenjeza anthu,"Tsopano Iye akabwera kumeneko Sabata yotsatirayo, ndipo, pamene Iye abwera, inu musamumvetsere Iye.Tsopano, mwina Inu mutha kupita ndikukakhala apo, koma osakapere tcheru chanuku zomwe Iye anena, chifukwa Iye sali wagulu lathu. Iye ndi otaidwa kunja. Iye alibe khadi la chiyanjano. Iye ngakhale pe. . . pepala la bungwe ndi iye. Iye alibe chirichonse ngati chimenecho."

"Iye ndichiyani."

"Mnyamata wina osokoneza yemwe anabadwirakumusi kuno, obadwa wachigololo, cha pakwawo pa akalipentala, ku mai winaanakhala ndi pakati pa Iye iwo asanakwatirane, ndipo iwo akuyetsetsa

kuchibisachintchucho motero ndi chinthu chauzimu.” “Ife tikudziwa kuti, pamene Mesiyayoabwera, Iye adzabwera kutsika kuchokera mu njira za Kumwamba ndipo ndikupita kwa wamsembe wathuwamkulu ndipo ndikunena kuti, 'Ndilipano Ine, Kayafa.'”

Koma ife tikupezakuti Iye sanazipange izo motero, chifukwa izo sizinalembedwe mu Mawu mwa njiraimeneyo. Izo zinali miyambo yopangidwa ndi anthu zomwe zinapangitsa iwo kutiakhulupirire chimenecho. Mawu anali atanena kuti Iye akanadzabwera basi munjira yomwe Iye anabwerera. Ndipo Iye anaima apo, akuwerenga Mawu, nanena kwa iwo,“Lero Lemba ili lakwaniritsidwa pamaso panu.” Ndipo komabe iwo analepherakumuona Iye, kapena kumizindikira Iye, monga iwo anachitira mu mibadwo inayonse.

25 Nowaakanakhoza kunena chinthu chomwecho, tsiku lomwe iye analowa muchombo ndipokhomo linatsekedwa. Mose akanati akweze m'mwamba zenera pamwamba pa chombocho,nayang'ana kunja pa osonkhana . . . Kumbukirani, Mulungu ndi yemwe anatseka khomo. Ndipo Iye akanati anene kuti, “Lero Lemba ililakwaniritsidwa pamaso panu,” koma inali nthawi itawathera iwo pamenepo. Iyeanali atalalikira kwa zaka makumi khumi ndi awiri, kuti ayetsetse kuwalowetsaiwo mu ngalawayo yomwe iye anali ataimanga, kuwauza iwo kuti Lemba linati, “PAKUTI ATERO AMBUYE, kugwa mvula,” koma iwoanadikira nthawi yaitali. Koma Nowa mophweka, akananena kuti, “Lero, Lero,Lemba lakwaniritsidwa.”

Mose,tsiku lomwelo lomwe mtambo wamoto unatsika pa phiri la Sinai ndipo anaperekera umbonipa umboni wake, Mose akati anene kuti, “Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.”

Mose,inu mukudziwa, anali munthu wa Mulungu woitanidwa, mneneri. Ndipo pamene iyeankaitanidwa, pokhala mneneri, iye anayenera kukhala ndi chomuchitikira chaUzimu. Kuti iye akhale mneneri, iye anayenera kuti akumane ndi Mulungu maso ndimaso ndi kuyankhula ndi Iye. Ndipo chinthu china, chomwe iye ananenachinayenera kuti chichitike, kapena palibe wina yemwe akanakhozakumukhulupirira iye. Kotero palibe munthu yemwe ali ndi ufulu adzitchule yekhamotero mpaka atayankhulana maso ndi maso ndi Mulungu, mbali ya kuseri kwachipululu kwina kwake, kumene iye mwini anakomana ndi Mulungu. Ndipoosakhulupirira Mulungu onse a pa dziko sakanakhoza kuchilongosola icho ndikuchichosa mwa iye; iye anali pamenepo, iye ankadziwa kuti icho chinachitika. MKhristu wina aliyense ayenerakukhala ndi chomuchitikiza chimenecho iwo asanayankhule chilichonse chazakukhala MKhristu. Chokuchitikirani chanu chomwe!

26 Inendinayankhula ndi mzukulu wanga wamamuna, posachedwapa, m'nyamata wachicheperewaChikatorika yemwe anati, “Malume a Bill, ine ndathamanga uku ndi uko, kupitakulikonse kuyetsetsa kuti ndipeze chinachake .” Usiku utatha usiku wina, misonkhano iyi isanayambe iye wakhala akulira.Ndipo nthawi yausiku, wakhala akulota maloto oti akubwera kudzalowa,akuthamangira ku guwa, komwe ndimalalikira, ndikumalapa kuti wakhalaakulakwitsa.

Inendinati, “Melvin, palibe kanthu komwe iwe ukuyesera kupitako, ndi mipingoingati yomwe iwe uti ujowine. Ndi 'matimuone Maria,' angati uti unene, kapenandi madalitso angati omwe iwe ulandira kuchokera kwa munthu, iwe uyenerakubadwanso mwatsopano mwa Mzimu wa Mulungu. Icho ndi chinthu chokhacho chomwechingakhutitse mtima wa munthu.

Ichondi, ine ndikudziwa kuti iwo ali ndi chongolowetsa m'malo mwake, lerochakukhala obadwanso mwatsopano, basi kungogwirana chanza ndi mulaliki ndikuikadzina lanu pa bukhu. Koma, abwenzi icho ndi nthano chabe. Icho sichoonadi chaM'baibulo. Ngati icho chikanakhala, machitidwe a Atumwi, mu mutu wachiwiri,zikanawerengedwa motere, “Pamene tsiku la Pntekoste linafika kwathunthu, abusaanatuluka nagwirana manja ndi anthu.”

Komalimati, “Pamene tsiku la Pentekoste linafika kwathunthu,” pakukhazikitsidwa kwampingo, “Apo panabwera mkokomo kuchokera Kumwamba ngati mphepo yothamangayolimba, ndipo anadzadza mnyumba monse momwe iwo anali kukhala.”

Umo ndi momweMzimu woyera unabwerera pa nthawi yoyamba. Umo ndi momwe Iwo umabwerera nthawizonse kuyambira nthawi imeneyo. Iye ndi Mulungu, ndipo samasintha.

Tsopano, izizi zimaphunthwitsaanthu. Iwo anati, “Izo zinali za tsiku lina.”

27 Chabwino,Iye ali yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zonse. Nthawi zonse pamene mpingoukalandira Mzimu Woyera, Iwo nthawi zonse umabwera monga unabwerera nthawiyoyambayo, pansi pa zolembedwa zomwezo, Machitidwe 2:38 sizinasinthepo, sizidzasintha.

Mongazolemba za dokotala za matenda. Iye amalemba zolemba za matenda, a dokotalaamatero. Ndipo amatengera izo kwa wina yemwe amapanga za mankhwala komaasanaphunzitsedwe, ndipo iye amaikamo mankhwala ochuluka mwa icho, izozimakhala zofooka motero kuti izo sizimakuchitiranso ubwino; ngati iye aikapoizoni ochuluka kwambiri mwa iwo, izo zikuphani inu. Izo ziyenera kulembedwabasi monga mwa dokotala. Ndipo zolembedwa za dokotala pa za momwetingalandirire Mzimu Woyera zaperekedwa kwa ife ndi Dokotala Simon Petro, patsiku la Pentekoste.

“Ine ndikupatsani inu zolemba za dokotala. Lapaniwina aliyense wa inu, ndipo mubatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu kuloza kuchikhulupiriro cha machimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.Pakuti zolemba za dokotala izi zaperekedwa kwa onse akutali, ndi kwa onse iwoamene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.” Zolembedwa za muyaya izo!

28 Moseanali atakhala nacho chochitika ichi Iye anapita kumusi mu dzikolo ndipo iyeanayamba kuwauza anthu, “Ine ndinakumana ndi Mtambo wa moto. Iwo unali muchisamba choyaka. Ndipo Iye anandiuza ine kuti ndikuuzeni inu. 'INE NDINE YEMWE NDIRI INE. Pita kumusi; Inendidzakhala ndi iwe. Tenga ndodo mu dzanja lako ndipo uloze nayo ku dziko laAigupto; chili chonse chomwe iweungapemphe, icho chidzachitidwa.'”

Chabwino, mwinankutheka kuti wansembe wina anati, “Zankutu!”

Komapamene iwo anaona Mfundo zenizeniza ichi, kutenga zikuchitika, iwosanathe kuzisunga izo mopitirira. Iwo amadziwa kuti Iye atumizidwa ndi Mulungu.

Ndiyeno,ngati Mose anati anaona izo nachitira umboni kwa icho kuti ndi Choonadi, koteroMulungu ndi okakamizika, ngati icho chili Choonadi, kukazindikiritsa ndikutsimikizira Mawu a munthu ameneyo, kukhala Choonadicho. Izo ndi zoona.

NgatiYesu akanaima pamenepo ndipo ndikuwerenga, tsiku limenero, “Lero Mawu awaakwaniritsidwa pamaso panu,” Mulungu ndiwokakamizidwa kuwapanga Mawu amenewokuti achitike.

Ifetikuima pano usiku uno ndikunena, kuti, “Yesu Khristu ndi yemweyo dzulo, lero ndi kunthawi zonse.” Mulungundiwokakamizidwa kuti atsimikizire izo kuti zikhale choncho, chifukwa awo ndiMawu Ake. Tsopano, kodi izo zimachita chiyani? Izo zimatengera chikhulupiriro,mu kukhulupirira Awo. Zimatengera chikhulupiriro mukukhulupirira Mawu Ake, kutiIwo ndi Choonadi.

29 Zindikiranichomwe chinachitika pamene Moseanawatulutsa ana, ndi ena onse anamutsatira iye. Iwo amene sanamutsatireanatsala mu Aigupto. Koma iwo amene anamutsatita Mose, pamene iwo anatuluka muNyanja Yofiira nalowa mu chipululu, Mulungu anatsika pa phiri la Sinai. Mtambowa Moto uja unapangitsa phiri lonse kuyaka moto, ndipo Liwu linalakhulakutuluka m'menemo ndipo Mulungu anapereka Malamulo khumi aja. Mose akanakhozakuyenda pamenepo pamaso pa anthu nati, “Lero Lemba ili lomwe ndakhalandikukuuzani, monga mneneri Wake lakwaniritsidwa tsiku ili. Ine ndinakuuzani inukuti Mulungu anakomana nane, ndipo pamwamba apo pa chitsamba choyaka, mu Mtambowa Moto, ndipo Iye ananena ichi, 'Ine ndidza . . . Ichi chidzakhala chizindikiro. Iweudzawabweretsa anthu awo kawirinso pa malo awanso.' Ndipo apo pali Mulungu, muMtambo wa Moto omweo omwe ine ndinakuuzani kuti ali m'menemo, Utaima apopamwamba pa phiri. Lero uneneri uwu wakwatiritsidwa. Apa Iye ali kutiakatsimikizire kuti zinthu zomwe ndanena ndi Choonadi.”

Mulunguatipatse ife amuna ambiri ngati awo, omwe ali owona mtima ndi odzipereka, ndikulankhula Choonadi, kuti Mulungu wa mphamvu zonse akanatsimikizira kuti MawuAke akadali Choonadi! Iye akadaliyemweyo dzulo, mpaka kale. Chifukwa chiyani Iye sakanachita izo? Iye analonjezakuchita izo.

30 Yoswamwina analankhula mofanana, tsiku lomwe iye anabwerera ku Kadeshi Baneya komwe iwoanali atayenda motalika mu chipululu. Iwo anali kukayikira dzikolo kukhalamtundu wa dziko lomwe Mulungu anatilidzakhala. Koma Mulungu anawauza iwo kuti linali dziko labwino, ilo linaliloyenda mkaka ndi uchi. Ndipo Yoswa ndi Calebu anali awiri okha omweakanakhulupirira izo, pambali pa khumi enawo omwe anachoka. Pamene iwoanabwerera, iwo anali ndi umboni; iwo anali ndi phava la zipatso zampesa lomweamuna awiri amphamvu okha akanatha kunyamula.

Yoswandi Calebu akanatha kuima chapamenepo ndikunena, “Lero Lemba ililakwaniritsidwa. Apa pali umboni kuti ilo ndi dziko labwino.” Zedi. Chifukwa chiyani? “Apo pali umboni otiilo ndi dziko labwino. Iwe umazipeza zinthu ngati zimenezo kuti, ku Aiguputo? Kunalibemalo ngati amenewo. Koma Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.”

Iyeanakhoza kunena chinthucho, chimodzimodzi, pamene iye ananenera nati makoma aYeriko akanadzagwa pansi iwo atatha kuguba chozungulira iwo kasanu ndi kawiri,masiku asanu ndi awiri, kasanu ndi kawiri patsiku. Ndipo pamene iwo anaguba pozungulirakwanthawi yomaliza, makomawo anagwa pansi. Yoswa akanakhoza kuimirira ndikunenakuti, “Lero, kapitao wamkulu wa gulu lankhondo la Ambuye yemwe anandiuza inemasabata apitawo kuti zidzachitika motere, Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.” Apoanagona makomawo, onse ali pansi pa nthaka. “Bwereni, tiyeni tipite tikantengeiwo. Iwo ndi wathu.

Lero Lemba ililakwaniritsidwa. Ndi zodabwitsa bwanji, anthu a Mulungu anali ataimira zinthuzomwe zinali zolondola!

31 Aisrayeli,pa mtsinje pamene analandira dziko, anapita uko. Kodi iwo akanachita izomotani? Iwo unali mwezi wa Epulo. Madzianali atasefukira chifukwa chipale (chisanu) chinali chikusungunuka, uko kuYudeya. O, ndi mtsogoleri otani yemwe anaoneka osadziwa ngati momwe amaonekerangati Mulungu

anali, kuti anabweretsa anthu Ake kumeneko, mu mwezi wa Epulo,pamene Yordano anali atadzadza kuposa nthawi zonse.

Nthawi zina . . .Ine ndikanakhoza kuima apa, ngati ndikanakhala ndi nthawi, kuti ndikupatseniinu basi kokuthandizani kakang'ono. Nthawi zina inu mutha kukhala pamenepo ndimatenda akhansala, kapena inu mutha kukhala ndi nthenda; inu mukuganiza,"chifukwa chiyani, ine pokhala MKhristu, ndikanakhala motere? Chifukwa chiyani ine ndili oti ndikanakhalamotere, ngati ine ndili MKhristu?"

Nthawi zinaMulungu amalora zinthu kufika pochita mdima kwambiri kuti mpaka iwe osathakuona, pozungulira, kapena kwina kulikonse, ndipo kenako Iye amabweranakupangira iwe njira kupyolera mu ilo, kuti uthe kunena, "Lero Lemba ili likukwaniritsidwa,chomwe Iye analonjeza kuchita."

32 Iyeanawalora ana achihebri aja mpaka kukalowa mu ng'anjo ya moto. Iwo anati,"Mulungu wathu ali ndi kuthekera kutiwombola ife ku ng'anjo iyi ya moto. Komasizingathekebe kuti ife tipembedze fano lanulo." Pamene io anatuluka menemo,fungo la moto lili pa iwo . . . panalibe fungo la moto kani, pa iwo; Iwoakanakhoza kunena kuti, "Lero Lemba ili lakwaniritsidwa."

PameneDanieli anatuluka kuchokera mu dzenje la mikango, Iye akanati alakhulechimodzimodzi.

YohaneM'batizi. Patatha zaka mazana anayi za chiphunzitso cha chipembedzo,mzosadabwitsa kuti mpingo unali mu chisokonezo nthawi imene ija! Pamene Iyeanaoneka mu chipululu, Yordaniyo, Iye akati angoima apo pa mbali pa mtsinje,monga anachitira, ndipo nati, "Lero Lemba ili, Yesaya 40, lakwaniritsidwa.

33 Momweine ndingati ndiime apa ndikukuuzani inu chomwe wansembe wakale uyo anandiuza ine! Anati, Mwana wanga, iwe sunatsirizeuthenga uja."

Ine ndinati,"khalani bata."

Iye anati, "Iweukutanthauza kuti awo achiPentekosite sakuchiona icho."

Inendinati, "Ai."

Iyeanati, "Ine ndachiona icho." Ndipo wamsembe wachiKatolika, naponso! Uhu-uhu. Iye anati, "Chifukwa chiyani iwe sunapitirize?"

Inendinati, "khalani bata."

Iyeanati, "Mulungu Alemekezeke! Ine ndachiona icho."

Ndipocha munthawi yomwe Mzimu Woyera unagwa pa m'chemwali wake, yemwe anakhala kunjauko mu msonkhano. Ndiye iye anaimirira nalankhula mu malilime achilendo, ndipo anapereka kutanthauzira kwachinthu chomwecho chomwe wamsembe ndi ine tinali kukambirana, pa guwa. Mpingoonse, malo onsewo panabuka chiphokoso. Zinapitirira mpaka mu msonkhano wa OralRoberts sabata yatha, kapena sabata yapitayo, pa msonkhanowo. Momwe wamsembeuja atakhala pansi pa Mzimu Woyera, zinaululidwa kunja uko kupyolaera mwamkazi, Mchemwali wake inendikukhulupirira anali, pa zomwe zinali kuchitika apo pa guwa, ndipo ndikuululachinthu icho chomwe ife tinabisa.

Oralomwe ife tikukhalamo, Lero Lemba ili lakwaniritsidwa. Lero kuwala kwa nthawi yamadzulokwafika, ndipo ife tikulephera kuchiona Icho.

Zindikirani.

34 Yohane anati, "Lero ine ndine 'Liwu la iye wofuula mchipululu,'monga ananenera mneneri Yesaya. Konzaninjira ya Ambuye!"

Iwosankamvetsa icho. Nati, "O, iwe ndiwe Yesu iwe ndiwe-iwe ndiwe Khristuyo," kani.

Iyeanati, "Ine sindine Khristuyo." Iye anati, "Ine sindine woyenera kumasulazingwe za nsapato zake. Koma," iye anati "Iye waima pakati panu penapake," Pakuti iye anali otsimikiza kuti Iyeakanadzakhala pamenepo. Iye akanadzakhala mu tsiku lake, chifukwa Mulunguanamuuza iye kuti iye akanadzafotokozera Mesiyayo.

Tsikulina mamuna wachinyamata anabwera akuyenda kubwera kumeneko, ndipoamaoneka ngati panali kuwala pamutu pake, chidzindikiro. Ndipo iye anafuula,"Taonani Mwanawankhosa wa Mulungu! Lero Lemba ili lakwanirisidwa pamaso panu."

Zedi.

35 Patsiku la Pentekoste, momwe Petro anaima nawarenga Lemba, la pa Yoeli 2:38. Pamene, iwo anali akuwaseka, anthu awa.Iwo ankabwebweta pa chinthu china chake. Baibulo linati, "Malirime ogawanika." Kugawanika ndi lirime "lolekana", osayankhula kanthu,basi kumangobwebweta. Akuthamanga mozungilira

ngati gulu la anthu olezera!

Iwoonse anati, "Chabwino, anthu awa aledzera. Tawaonani, taonani momwe iwoakuchitira, momwe azimayi ndi azibambo awo. Iwo asokonezeka," linatero gulu ilola chipembedzo la tsiku ilo.

Petroanaimirira pakati pawo nati, "Amuna inu Abale, inu akukhala mu Yerusalemu, ndiinu akukhala mu Yudeya, Ichi chidziwike kwa inu kuti awa sanaledzere, monga inumuyesa, poona kuti ili ndi Ora lachitatu la tsiku. Koma ichi ndi chija chomwechinalakhulidwa ndi mneneri Yoeli, 'ndipo kudzali m'masiku otsiriza, kutindidzathira cha Mzimu wanga pa thupi lirilonse.' Lero Lemba ililinakwaniritsidwa." Mtheradi.

36 Lutheranali mu nthawi yake. Wesley anali mu nthawi yake. AchiPentekoste anali munthawi yawo. Palibe chomwe chinali kunja kwa dongosolo.

Tsopanoine ndikukufunsani inu kuti mulingalire za m'badwo ndi nthawi yomwe ifetikukhalamo tsopano, ndi Mawu olonjezedwa a lero. Ngati kumbuyoko mu m'mibadwoinayo, anthu amakhoza kunena kuti, "Lero Lemba ili," "Lero Lemba ili," ndiyeno bwanji nanga Lemba la tsiku ili? Ndi chiyani chomwe chalonjezedwa kwa tsiku lalero? Kodi ife tayima pati? Kodi ndi ora lanji lomwe ife tikukhalamo; pamenenthawi ikupita, nthawi ya sayansi, mphindi zitanu isanafike pakati pa usiku?

Dzikolikunjenjemera. Mpingo uli pa kama la chivundi. Palibe aliyense yemwe akudziwapomwe iwo aimapo. Ndi nthawi yanji ya tsiku yomwe iyo ili? Nanga bwanji Lembala Lero?

Zikhalidwe za mpingo, kapena, zikhalidwe za mpingolero!

37 Mudziko, ndale, machitidwe athu a dziko, ali basi owola monga angakhalire. Inesindine wandale. Ine ndine MKhristu. Koma, ndilibe nazo ntchito kuti ndidzinenaza ndale, koma ine ndikungofuna basi kunena kuti iwo ndioola pa mbali zonse.

Inendinavota kamodzi, iyo inali ya Khristu; ine ndiyenera kupambana. Mdierekeziyoanavota motsutsana ndi ine, ndipo Khristu anandivotera ine; zinatengera kutindi mbali iti yomwe ine ndikuponyera voti yanga. Ine ndine okondwa kuti inendinaponyera voti yanga Iye; Liloreni dziko linene zomwe likufuna. Inendidakakhulupirirabe kuti Iye ndiyemweyo dzulo, lero, ndikunthawi zonse. Iyeadzadzitsimikizira izo. Iye mtheradi adzatero. Mtheradi.

Iwoakupitirirabe mu ziwawa, kusokonekera kwa achichepere! Tapenyani fuko lathu,lomwe kale linali duwa la dziko lapansi. Ufulu wathu waukulu wa demokalasi unapangidwakumbuyo uko mu-mu . . . pakulengedzedwa kwa ufulu odzilamulira. Ndipo kulengezakwa ufulu odzilamulira kunasainiridwa, ndipo pamenepo ife tinakhala ndi ufuluwa demokalase. Ndipo makolo anthu akalewo, ndi zinthuzo zomwe iwo anachita; ifetinakhala ndi fuko lopambana. Koma tsopano ilo likuola, ndi kulakatika,ndikugwedezeka, ndi kutaya zonse. Ndipo kumayetsetsa kuwadula anthu misonkho,kuti apeze ndalama zoti atumize uko, kuti agule ubwenzi kwa adani awo; iwoakuziponyera izo pamaso pathunso. Nkhondo yoyamba, nkhondo yachiwiri, komabekumasendeza ku nkhondo yachitatu. Ndithudi. Ndale zaola, zavunda, kuola mpakapa phata. Basi ndendende zomwe Mateyu 24 ananena kuti zikanadzakhala, "Fuko lidzalimbanandi fuko, ufumu kutsutsana ndui ufumu." Zinthu zonsezi zikanati zizachitike.Tiyeni tilingalire za ichi tsopano.

Chabwino.

38 Zindikiranichina, kuchuluka kwa kafukufuku wa za sayansi. Tsopano, nthawi ina, basi . . .Agogo anga aamuna anapita kukawaona agogo anga aakazi, pa ngolo. Tsopano ndindege ya jeti, komanso ngakhale chozungulira kupita mumlengalenga, kupita maloa kunja kwa mumlengalenga. Izo ndi zopambana… Bwanji; ndani uyo ananena izi?Daniele 12:4, anati, "Chidziwitso chidzachuluka mu masiku otsiriza." Ifetikuona ora lomwe tikukhalamo.

Zindikiranitsopano zi-zikhalidwe za dzikoli, chikhalidwe cha sayansi. Ndipozindikiraninso, lero, mu machitidwe athu a za maphunziro. Tsopano musayetserekuzikana izi. Ine ndili ndi zolembedwa m'manyuzi pepala, kuphunzitsa kugonana m'matcha . . . mu masukulu athu, kwa anaophunzira a ang'ono kuti adzigonana ndikuona ngati angathe kulumikizana mudziko. Inde, bwana.

Nangabwanji mu unsembe wathu? Usiku uno ine ndinapeza kachiduswa ka pepala. Uko ku LosAngels, California, za komwe gulu la azilaliki, ABaptisti, Pulesibeteriani azitumiki,anabweretsa gulu la anthu ogonana amuna okha m'menemo ndikumagonana amuna okha,mkumati iwo amayetsetsa kuti awakopere iwo kwa Mulungu. Pamene ilo ndi limodzila matemberero a ora lino, Chisodomu! Ndipo ngakhale lamulo linawamanga iwo.

39 Ndiyenoife tili pati? Kachitidwe kathu konse kaoleratu kuchokera pansi pathu. Inendikuona kuchuluka kwa mchitidwe ogonana amuna okha kudutsa United States yonsezaonjezeka ndi makumi awiri kapena atatu pa zana kuposa chaka chatha.Tangoganizani za izo, mamuna kugonana ndi mamuna, basi ndendende mongaanachitira mu Sodomu.

Kuchulukakwa milandu yoopsa, kusokonezeka kwa achichepere! Kodi ndi ora lanji lomwe

ifetikukhalamo? Lero Mawu awa a uneneri akwaniritsidwa.

Dzikola chipembedzoli, mpingo iwo omwe, mpingowo, mpingo omwe watulutsidwa, omwe ifetimautchula mpingo otulutsidwa, m'badwo otsiriza wa mpingo, m'badwo wa mpingo wachiPentekosite,iwo ali pati? Iwo uli mu Laodikiya, monga momwe Lemba linanenera.

Leroiwo alekerera. Azimayi awo akuvala mwa theka. Amuna awo aku . . . Ndi chinthuchoopsa kwambiri. Ena a iwo anakwatirapo katatu kapena kanayi, koma ali mu gulula madikoni ndi zinthu zonse. Iwo atayilira, nabweretsamo chinyengo, chifukwaiwo akhala mu mabungwe ndipo atenga malo ndi dziko. Ndipo, lero, iwo ali ndinyumba zabwinoko kuposa zomwe anakhalapo nazo. Malo ena, m'modzi wa iwoakumanga malo olankhuliramo a madola zikwi makumi asanu, madola zikwi makumiasanu. Pentekosite! Iwo ankakhala pangodya, zaka makumi awiri ndi zisanu zapitazo, akumenya zisakasa. Anati, "Ife . . ." Chifukwa, Malemba anati, mu Chivumbulutso 3,kuti inu muli "'Wolemera,' anati, 'Inendine wolemera. Ndimakhala monga mfumumkazi. Ine sindisowa kanthu.' Ndipo iwe sudziwa kuti ndiwe watsoka, omvetsachisoni, osauka, wamaliseche, wakhungu, ndipo iwe sudziwa icho!" Lero Lemba ililakwaniritsidwa pa maso panu. Ameni!

Ameniamatanthauza "zikhale chomweho." Inesindikuzipangira ameni ndekha, koma ine ndikutanthauzakuti ndikukhulupirira kuti izo zili Choonadi. Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.

40 Mpingowa chiPentekosite uli mu chikhalidwe cha Laodikaya. O, iwo adakadumphabenamakuwa, ndikumapitirira pamene nyimbo zikuimbidwa. Pamene nyimbo zisiya kuimba,kapena nyimbo zachikunja zomwe ena a iwo amasewera ndipo ndikumaazitcha izo Chikhristu,ndipo pamene izo ziima, ulemerero onse umachoka. Mwaona?

Ngatiuko kuli kupembedza kwenikweni kwa Mulungu, apo palibe mawenzulo okwanira ndipozokwanira-mphamvu zokwanira mu dziko kuti ziimitse icho. Pamene izo zibwerakwenikweni kuchokera kwa Mulungu, izo sizimatengera nyimbo kuti zikamenyedwe.Izo zimatengera Mzimu wa Mulungu kuti utsikire pa izo Uwo ndi omwe umachitaizo. Ndipo iwo aiwala kale Iwo, chifukwa iwo apatula mphatso ya Mzimu Woyera,"umboni weniweni wa kulankhula mu malirime." Ndipo ine ndamvapo ziwanda ndiafiti akulankhula mu malirime.

MzimuWoyera ndi Mawu a Mulungu mwa iwe. Omwe umadzizindikiritsa Iwo mwini pakuvomereza Mawu amenewo. Kunja kwa izo, iwo sungakhale Mzimu Woyera. Ngati iwounganene kuti ndi Mzimu Woyera, ndikumakana limodzi la Liwu la M'Baibulo ilo,iwo sungakhale Mzimu Woyerawo. Uwo ndiye umboni kaya inu mukhulupirira kapenaai.

41 Zindikiranichizindikiro china chachikulu. Ayuda ali ku dziko lakwawo; fuko lawo lomwe,ndalama yawo yomwe, membala wa bungwe la United Nations. Iwo ali ndi asilikaliawo a nkhondo. Ali ndi chirichonse.

Iwo ali ku dzikola kwawo; chimene, Yesu anati, "phunzirani fanizo la mtengo wa mkuyu! Apo iwoali, abwerezanso kudziko la kwawo lomwe. Lero Lemba ili lakwaniritsidwa,

Ayuda ali kudziko la kwawo. Lero Lemba ili lakwaniritsidwa, M'badwo wa Laodikaya. LeroLemba ili, Mateyo 24, wakwaniritsidwa. Dziko liri mu Chivundi, chinthu chonseicho; mafuko kuukirana ndi mafuko, zivomerezi ponseponse, akavuluvulu aakuluakubwera ku musi, kugwedeza mafuko, ndi zina zotero, mavuto aakulu ponseponse.Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.

42 Tsopanoife tapeza chikhalidwe cha dzikoli. Ife tikuona komwe mpingo wabwinowo, bwino .. . Bungwe, chipembedzo ife tikuonapomwe iwo ali. Ife tikuona pomwe mafuko ali. Ndipo ife tikuona kuti tsiku ilimalonjezo awa akwaniritsidwa. Tsopano, koma mu tsiku ili pabwera mbewu yapamwamba ya Chifumu ya Abrahamu. Izo ndi ndendende izo ziti zikhale, zikhalaMkwatibwi wa Chifumu kwa Mwana olonjezedwa, wa Chifumu. Monga inendinalakhulira usiku watha, iyo siikhala mbewu yachilengedwe, iyo ikhala mbewuyauzimu. Apo pakhala Mkwatibwi wa uzimu akudzuka, amene ati akhale Mbewu ya Chifumuya Chikhulupiriro chachifumu cha mwana wa Chifumu wa Abrahamu. Iye (Mkwatibwi) abwera poonekera mu masikuotsiriza, ndipo nthawi ndi malowo ndi lonjezo limene laperekedwa kwa Iye. Mongamwa Malaki 4, Lemba, payenera kudzuka Uthenga omwe ugwedeze mitima ya anthukubweranso kwa atate achipositoli kawiri.

Apo padzuka wina poonekera,mu mphamvu ya Eliya, yemwe ati adzuke poonekera; Mamuna wa mu chipululu yemweati atuluke,ndipo adzakhala ndi Uthenga omwe uti upite molondola kubwera kuMawu kachiwiri. Ilo ndi ora lomwe ife tikukhalamoli.

43 Ndiyeno,lingalirani tsopano, ine ndikukufunsani inu pa ora ili, anthu inu pano a mu Jeffersonville.Mu chaka cha 1933, Kuwala kwa Uzimu kuja komwe kunagwa uko kumusi ku mtsinje,tsiku lija pamene ine ndinabatiza anthu mazana asanu mu Dzina la Yesu Khristu,ndili ngati m'nyamata wa zaka makumi awiri. Kodi Iwo unanena chiyani,Jeffersonville? Kodi Icho chinali chiyani uko kumapeto kwa msewu wa Spring pamene wa nyuzi pepala ya Courier Journal, ine ndikukhulupiriraiyo inali Ya Louisville Herald, inalindi cholembedwa pa icho? Icho chinapita naponso modutsa a Associated Press, mpaka kulowa mu Canada.

Dotolo Lee Vayle anadulaicho kuchokera pepala, uko ku Canada, mu 1933.

Pameneine ndinali kubatiza munthu wa khumi ndi zisanu ndi ziwiri, pansi pa Mboni iyi,ndipo inu mukudziwa nkhani yonse iyo. Ndipo pamene ine ndinali kuima pamenepo,ndikubatiza munthu wa chikhumi ndi zisanu ndi ziwiri uyu, kuwala kunatsikakuchokera Kumwamba, kukuwaliza cha pansi pamwamba apo, monga Nyenyezi ikugwakuchokera Kumwamba. Liwu linati, "Monga Yohane M'batizi anatumizidwakukatsogolera kubwera koyamba kwa Khristu, Uthenga wako udzatsogolera kubweraKwake kwa Chiwiri, mu dziko lonse." Lero Lemba ili lakwaniritsidwa."

44 [Osonkhana akusangalala-Mkonzi.] Lero! (osonkhana akusangalala mopambanandikumayamika Mulungu.) Mulunguanalonjeza izo. Chinachitika ndi chiyani? Lero izo zapita ku dziko lonse. Ndipopamene Mulungu anatsika nabwera uko ndipoanati kuti, pamene ine ndinali mnyamatawam'ng'ono mu chisamba choyaka, kapena muchitsamba uko, chikuyaka ndi Mtambo waMoto kumtunda uko ku malo a Wathen pa Utica Pike; nditanyamula madzi ku mbuyouko, kuchokera pa khola kuwala kwa mwezi kwa yaziyazi, inu mukudziwa Choonadi chaizo.

Iye anati, "Iweusadzasutepo fodya, usadza mwepo, kapena kuononga thupi lako, pakuti palintchito yoti udzagwire ukadzakula."

Ine ndikuchitiraumboni kuti icho ndi Choonadi, kuti ine ndinaona Icho. Ndipo Mulungu, monga Iyeanachitira ndi Mose, anayankhula pamaso pa osonkhana ku musi uko, ndipo anati,"Ichi ndi Choonadi." Lero Lemba ili lakwaniritsidwa pakati pathu.

Onanizomwe Iye analankhula pa zakuzindikira za pansi pa mtima, ndipo momwezikanadzakhalira; kuyambira pa kusanjika manja pa iwo, mpaka kukudziwa zinsinsizapansi pamtima. Lero Lemba ili lakwaniritsidwa pa maso pathu pomwe.

45 Malonjezoawa omwe anapangidwa.

Zindikirani,malonjezo onse awa anatsimikiziridwa ndikukwaniritsidwa ndi Mulungu wa lonjezoyo.Tapenyani, zapachikidwa mu Washington, D.C., usiku uno, chithunzi cha Mngelo waAmbuye! Monga George J. Lacy, wamkulu wa zopima dzala ndi zolemba ku FBI muboma la United States, anachifufuza Icho kuchokera ku Houston, Texas, ndipoanati, "Ichi ndi chokhacho Chokhalapo chauzimu chomwe chinayamba chatengedwachithunzi mu dziko lonse." Iye anali oti adziwe; iye ndi katakwe yemwe alipo padziko pa nkhani zimenezo.

Zindikirani,Icho chapachikidwa apo, monga Choonadi, Mtambo wa Moto Omwewo omwe unatsogoleraAisarayeli ku mbuyo uko muchipululu. Iwo ukutsogolera lero, Uthenga wa mtunduOmwewo, wa, "Tulukanimo mu Igupto!" . . . ? . . . Lero Lemba ili lakwaniritsidwa. Inu mukudziwaUthenga omwe Iye ananena.

46 Tapenyanipa masomphenya a ku Tucson, zaka zitatu zapitazo, pamene ndimaimirira kuno apamu mpita. Pamene, zaka zisanu zisanachite izo, Iye anati, "Tsiku lomwe a mzindaadzakhome chikhomo patsogolo pa chipata chako, iwe udzatembenukira ku madzulo."Abale a ku kachisi wanga Omwe ali pano, akudziwa icho . . . icho-nthawi iyo.Uko nkulondola.

Ndipotsiku lomwe a Goynes ndi ena onse anali ku mtunda uko, ndipo nakhoma chikhomopansi, ine ndinati kwa mkazi wanga, "Pali china chake pa za ichi."

Iyeanati, "kodi ndi chani?"

Ndipoine ndinalowa mkati ndikukapenya mu bukhu langa laling'ono. Icho chinali apo.

Ndipom'mawa otsatirawo, cha m'ma 10 koloko, nditakhala m'menemo, mu chipinda changauko, pafupi 10 koloko, Mngelo wa Ambuye anatsika. Iye anati, "Pita ku Tucson.Iwe udzakhala cha kummawa kwa kumpoto kwa Tucson, ndipo kumeneko kukabweraAngelo asanu ndi awiri moundana zomwe ziti zidzagwedeze dziko lonse lapansilozungulira pa iwe." Ndipo anati, "Iweudzakauzidwa izo kuchokera kumeneko."

Ndiangati omwe akukumbukira chimenecho, kuno kumbuyo uko izo zisanachitike. (Osokhanaanena, "Ameni"-Mkonzi.) Pali amuna akhala pompano mu nyumba iyi usiku uno,anali kuima pomwepo pamene izo zimachitika. Ndipo anati, "Zisindikizo zisanundi ziwiri za zinsinsi zobisika za mu Baibulo lonse zidzatsegulidwa, ndikulikwaniritsa Chivumbulitso 10, kuti mu Uthenga wa Mngelo wa chisanu ndichiwiri zinthu izi zidzayenera kuchitika." Lero Lemba ili lakwaniritsidwa pamaso pathu. Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.

47 Chakachatha, nditaima pa malo omwewo, Bambo Woods apa ndi ine, tikukwera phiri, mumtundu wina wa m'mawa, akazi awo akudwala. Mzimu Woyera unati, "Tola mwala uliapowo. Uponye iwo m'mwamba. Pameme iwo ugwera pansi, unene, 'PAKUTI ATEROAMBUYE, pakhala chiweruzo chikukantha dziko lapansi.' Umuuze iye kuti iye awonadzanja la Mulungu, ma ora ochepa otsatirawo."

Inendinawauza Bambo Woods; Iye ali pano usiku uno. Ndipo, ndikuganiza, amuna asanundi atatu, kapena khumi, kapena khumi ndi asanu, amene anali apo pa nthawiimeneyo pamene izo zinachitika; M'mawa wake, pomwe ambuye anabwera mukamvuluvulu nang'amba phiriro pozungulira ife, nadula m'mwamba mwa mitengo nkumalendewera,nazipanga kuphulika katatu, ndipo anati, "Chiweruzo chikupita cha ku gombe lakumadzulo."

Patapitamasiku awiri kuchokera apo, Alaska anali pafupifupi kumira pansi pa nthaka.Ndipo kuchokera apo, kukweza ndi kutsika ku gombe, zophulitsa za chiweruzo cha Mulungumotsutsana ndi chotchinga chauzimu.

Apo pali kataniya chitsulo, po pali katani ya msungwi, ndipo apo pali chotchinga cha tchimo.

48 Chitukukochayenda ndi dzuwa; chomwechonso Uthenga. Izo zachokera ku m'mawa ndipo zapitakumadzulo, monga momwe dzuwa limayendera. Ndipo tsopano zili cha ku gombelakumadzulo. Icho sichingapitirirenso apo; ngati icho chingapitirire apo, ichochibwereranso kum'mawa kachiwiri.

Mnenerianati, "Kudzakhala tsiku lomwe silizakhala usiku kapena masana," tsiku lalolunda mvula yambiri kapena chifunga, basi zongokwanira kudziwa momwe ungajowinirempingo kapena kuika dzina lako m'buku. "Koma kudzakhala kuwala ku nthawiyakumadzulo." Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.

Lomwelo- D-Z-U-W-A lomwero lomwe limatuluka kum'mawa ndi D-Z-U-W-A lomwero lomwelimakalowa ku madzuro. Ndipo M-W-A-N-A yemweyo wa Mulungu yemwe anabwera ku m'mawa ndipo nadzindikiritsa Iyemwini ngati Mulungu owonetseredwa mnthupi, ndi M-W-A-N-A yemweyo wa Mulungu ku malowero a dzuwa kuno.Amene akudzizindikiritsa Iye mwini pakati pa mpingo usiku uno, Yemweyo dzuro,lero, ndi kunthawi zonse. Kuwala kwa kumadzulo kwa Mwana kwafika. Lero Lembaili lakwaniritsidwa pa maso pathu.

49 Kodiife tili pati mu m'badwo uwu wa Abrahamu? Kodi ife tili pati mu nthawi yaikuluiyi yomwe ife tikuimamo, ora lalikulu lomwe ife tikukhalamo? Masomphenya onseakwaniritsidwa. Bwanji paja pamene bwenzi mtumiki wam'ng'ono kuno, ku mpingoothandizana nafe wa paubale, Junior Jackson, anabwera akuthamanga kubwera kwa ife usikuumodzi, ine ndili pamenepo. Anati, "Ine ndinali ndi-ndi loto, M'bale Branham,lomwe likundisautsa ine. Ine ndinauza abale onse atasonkhana pa phiri." Ndipo anati, "Pamwamba pa phiri limeneli, inumumatiphunzitsa ife kuchokera ku zolembedwa zomwe zinali zitalembedwa,zimaoneka ngati, mu zolembedwa zina mu nthawi imeneyo zinali zitagobedwakuchokera mu tanthwelo. Pamene inu munatsiriza izo, zonse izo zinatsirizika,inu munatiuza ife, mumati, 'bwerani pafupi,' ndipo ife tonse tinasonkhanapamenepo." Anati, "Inu munafika kuchokera kwinakwake ndipo, zimaoneka ngati,inu munali ndi china chake ngati chokhapira ndipo munakhapa pa mwamba pa kapiramidi nkutsegula. Ndipo, pamene izo zinatero," anati, "thanthwe la tsangalabwilopanda zolembedwa pa ilo. Ndipo inu munatiuza ife kuti 'ziyang'anani umu apa.'Ndipo inu nonse … ife tonse tinayamba kuyang'ana." Anati, "Ine ndinatembenuzamutu wanga, ndipo ine ndinaona inu mukupita cholunjika ku madzuro, molimba basimonga mukanathera, molunjika ku malowero a dzuwa." Ndi angati omwe akukumbukiraizo? (Osonkhana anena, "Ameni."-Mkozi.)

50 Ndipoine ndinaima apo kanthawi kochepa mpaka Mzimu Woyera unaulula icho. Inendinati, "Baibulo lonse, muchuluka momwe ilo laululidwira kwa Munthu, kapyoleramu kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, ubatizo mu Dzina laYesu, ndi zina zonse izi, zomwe zaululidwa; koma apo pali zinsinsi zomwezabisidwa mkati, chifukwa Baibulo ndi losindikizidwa ndi zinsindikizo Zisanundi Ziwiri. Ine ndiyenera kupita uko kuti ndikapeze izo.

M'mawaumenewo pamene Angelo asanu ndi awiri aja anabwera pansi naphuritsa dzikolapansi, ndipo miyala inaulukira njira zonse, Angelo asanu ndi awiri anaimapamenepo nati, "Bwerera ku Jeffesonville, komwe iwe wachokera, pakutiZisindikizo Zisanu ndi Ziwiri za zinsinsi zisanu ndi ziwirizo zidzatsegulidwa."

Ndiife pano, lero, tikumvetsa Mbewu yaSerpenti. Mu masiku ochepa, ngati Mulungu alora, ife tidzamvetsa kulondolakwa Chikwati ndi Chilekaniro. Ndipozinthu zonse izi zomwe Mulungu watsegula, chisindikizo chili chonse, zinsinsikuchokera pomwe maziko a dziko. Ndipo ife takhala mu kusangalala, mu kukhalapokwa Madalitso Ake! Izo ndi zoona. LeroLemba ili!

51 ALife Magazine analemba za icho,"Kuwala kodabwitsa kozungulira kupita m'mwamba mumulengalenga pamwamba paTucson ndi Pheonix," mu njira yomweyo yomwe ine ndinakuuzani inu-pafupifupichaka izo zisanachitike, momwe izo zikanakhalira, ndipo monga chinthu chamakona atatu. Chithunzicho chapachikidwa mu tchalitchi ku musi uko. Inu omwemunagula magazine imeneyo muli nacho. Apa icho chinali, basi ndendende. Iwoanati, "Iwo anali ma mailosi makumi awiri ndi zisanu ndi ziwiri pamwamba, ndimamailosi makumi atatu kupingasa." Iwo sakumvetsa apobe chomwe chinachitika. Iwounaoneka mwachinsinsi ndipo unachoka mwachinsinsi.

KomaM'bale Sothamann. M'bale Gene Norman komanso Ine, tinaima pamenepo. Atatu ndiMboni. Monga Iye anatenga pamwamba pa phiri; Petro, Yakobo, ndi Yohane,kukapereka umboni. Anaima

pamenepo napenya icho pamene chimachitika, ndipokuchiona icho chikutsirizika. Icho apo chili, chitaima mumlengalenga; apobe,apo palibe chinyotho, palibe chinyezi kapena chilichonse choti chingapange chi-chifunga. Izozikanabwera apo bwanji? Awo anali Angeloa Mulungu akubwerera, atatha kupereka Uthenga wawo. Lero uneneri umene ujawakwaniritsidwa pakati pathu. Lero Lemba ili lakwaniritsidwa.

Penyani,Zisindikizo zisanu ziwiri zatsegulidwa. Kamvuluvulu ali ku gombe lakumadzulo.Tsopano, musachiphonye icho, monga iwo anachitara ku mbuyo uko.

52 Tsopano,tcheru chathu, tayandikira pang'ono ku tsiku lathu.

Kodi Lemba limatichiyani pa za lero, ndi pa za nthawi yomwe ife tikukhalamo? Yesu akulankhula .. . Ine sindikhala ndi nthawi yoti nditenge onsewo, koma ine ndikufuna kutinditenge chimodzi ichi tisanatseke. Yesu anati, mu Luka Woyera mutu wa 17,ndime ya 30. Yesu Khristu, Mawu Mwiniwake! Inu mukukhulupirira zimenezo.(osankhana anena, "Ameni."-Mkozi.) YesuKhristu, Mawu Mwiniwake, opangidwa thupianayankhula ndipo ananena chomwe Mawu akanadzakhala mapeto a nthawi, chomwechiti chidzakhale chizindikiro cha kutha kwa dziko. Iye anawauza iwo kuti fuko lidzaukirafuko limzake, koma Iye anati, "Monga zinaliri mmasiku a Sodomu, chomwechozidzakhalanso mu tsiku limene Mwana wa munthu adzakhale akuuluridwa." Tsopanopamene Yesu anabwera padziko lapansi, Iye anabwera mu dzina la umwana utatu.Mwana wa munthu, yemwe ndi mneneri; Mwana wa Mulungu; ndi Mwana wa Davide. Tsopano,Iye anakhala pano pa dziko lapansi. lyesanalakhulapo kuti lye anali Mwana wa Mulungu. Iye anati, "Ine ndine Mwana wa munthu." Yehovah Mwiniwake anamutcha Ezekieli ndi aneneri. "Mwana wa Munthu." Chifukwa, Iye amayenera kubwela kuti akakwaniritse Lemba ngati Mneneri. Mose anati, "Ambuye Mulungu wanu adzakudzutsirani inumneneri wonga ine.'' Icho ndi chifukwachomwe lye sakanakhala Mwana wa Mulunguuko, chifukwa Iye anali Mwana wa munthu.Iye . . . "Mawu anabwera kwa aneneri." Ndipo lye anali Mawu mu chidzaro chake. Mwana wa munthu, Mne- Mneneri wakulu . . . Osati mneneri wamkulu komaMulungu-Mneneri, "Chidzaro cha Umulungumu thupi chinali mwa lye." Kotero, Iye anati Mwana wa munthu.

Tsopano,kwa zaka zikwi ziwiri, Iye wakhala akudziwika kwa ife ngati Mwana wa Mulungu,Mzimu. Ndipo mu zaka chikwi, Iye adzakhala Mwana wa Davide, ali mu Mpando waChifumu. Ife tonse tikudziwa zimenezo, omwe timakhulupirira Malemba.

53 Tsopano,Yesu anati, basi chakumapeto kwa m'badwo wa mpingo uno omwe ife tikukhalamo,kuti, "Mwana wa munthu adzaululidwa kawiri mu machitidwe omweo omwe anachitira,monga momwe zinalili ku Sodomu." Penyani momwe, mwa mbiri anazipereka izo. Iyeanati, "Monga zinaliri m'masiku," choyamba, "a Nowa, momwe iwo ankadyera, kumwa, kukwatira ndi kukwatiwa."Kenako Iye anabweretsapo, kotsatira, chomaliza, kwa Mwana wa munthu, ku Sodomu.Chifukwa, apo Iye ankachita ndi aYuda; apa mu Sodomu, Iye akuchita ndi anthuamitundu. Apo anawamiza iwo onse m'madzi mu chiweruzo; kuno, pa a mitundu, Iyeanawaotcha iwo onse mu tsiku ku Sodomu. Uko nkulondola. Dziko la a mitundu linapsauko,

"Ndipo momwemozidzakhala pamene Mwana wa munthu adzaululidwa." Si madzinso ai, koma iwo udzakhala motoulendo uno. Yesu anawerenga kuchokera mu Genesesi 23 yemweyo yemwe ifetimawerengapo, pamene Iye anawerenga za Sodomu.

54 Tsopano,Ife tikuvomereza chikhalidwe chomwe chalankhulidwa, za chikhalidwe cha dzikocha chi Sodomu, Achisodomu, chikhalidwe cha Sodomu. Ife wina aliyense, adzati,"Ameni" ku icho. Ife tikukhulupirirazimenezo. Nkulondola uko. Ndipo chikhalidwe cha uzimu cha Laodikaya, mpingo wampingo wachithupi, ife tidzanena "Ameni" ku icho, ndi kuvomereza zizindikiro zawo.Ife tikudziwa kuti chizindikiro chirichonse chili pamenepo. Mpingo uli muLaodikaya. Ife tikudziwa zimenezo. (Osonkhana anena, "Ameni."-Mkozi.) Ifetikudziwa dziko liri mu chikhalidwe cha Sodomu. Nkulondola uko? (osonkhana anena, "Ameni."-Mkonzi.) Ife tidzavomereza chimenecho. Koma bwanjichizindikiro cha Abrahamu, amene akuyembekezera mwana walonjezo? Uyo analiwina. Kumbukirani, iwo anali ndi Sodomu kumbuyo uko; Iwo anali naye wanthengawawo. Ndipo Abrahamu anali naye Mthenga wake. Abrahamu anali nkudikira, tsikundi tsiku, kwa, pafupi chinthu chosatheka kuti chichitike. "Sarah makumi asanundi anayi, ndipo iye zana." Monga mwalonjezo la Mulungu, iye anali akudikirabe. Pakati pa kutsutsa konse, iye analiakudikira pa Mwanayo. Chomwecho ali okhulupirira owona akudikirabe Mwanaolonjezedwayo kuti abwerere!

Zindikirani, basimwanayo asanafike, apo panali chizindikiro chopatsidwa kwa iye. Kodichizindikiro cha mwana obwerayo sichiululidwa kwa Mbewu yachifumu ya Abrahamuyomwe ikudikira Mwana wa Chifumu, mofanana ndi momwe zinaliri kwa atateAbrahamu kwa mwana wa chithupi? (Osonkhanaanena, "Ameni."-Mkonzi.) Nkulondola uko? ("Ameni") Yesu amatero, apa muLuka Woyera 17:30, "Nthawi iyi isanafike, kuti, Mwana wa munthu akanatiadzaululidwe monga Iye anachitira mu masiku a Sodomu, chisanafike chiononge kocha Sodomu." Tsopano ifetikuyembekezera chizindikiro.

55 Tsopanotiyeni ife titenge zikhalidwe za nthawi monga zinaliri mu Sodomu. Zindikirani, iwoonse anapita mu Chisodomu, dziko. Ine ndikuganiza m'modzi wa awo akatswiri a masewero a pa kanema anaikachinthudzi, sikale kwambiri, ndipo ine ndinachiona icho, icho chinari, Sodumu. Ngati inu munachiona icho ndipopalibe chinthu chilichonse pa icho koma chimenecho, Tangochipenyani icho. Ichomtheradi ndi

chithunzi chabwino cha United States, lero, Hollywood, basindendende; mtundu wa diresi omweo ndi chilichonse chomwe iwo anachita ngatikulondola pamenepo; Malo omwera mowa akuluakulu ndi zina zonse, gulu la anthuakachipembedzo, otchedwa achipembedzo.

Zindikirani,ndipo Sodomu anali nayo mboni, ndipo anali mamuna otchedwa Loti, amene analiMzukulu kwa-kwa Abrahamu. Tsopano, Abrahamu sanapite kumunzi ku Sodomu, iye ndigulu lake. Iye anali nalo gulu lalikulu ndi iye, okwanira kumenyana ndi mafumukhumi ndi awiri ndi asilikali awo. Kotero, iye anali nalo gulu lalikulu ndiiye. Ndipo iye anakhala kunja uko pansi pa mtengo wa mthundu, tsiku lina,pamene china chilichonse sichinkayenda bwino kwa iye; Panalibe aliyense yemweamasamala za iye, koma iye ankagwiritsitsabe ku lonjedzanolo. Penyani tsopano,mwatcheru, ife tisanatseke. Pomwe iye anali chikhalire pamenepo, apopanatulukira amuna atatu, akuyenda kupita kwa iye. Awiri a iwo anapita kumusiku Sodomu ndipo analalikira Uthenga kwa iwo, woti atuluke, kwa Loti. Ukonkulondola? (Osonkhana anena, "Ameni."Mkonzi.) Koma M'modzi anatsala kwaAbrahamu. Zindikirani, Mmodzi yemwe anatsala kwa Abrahamu anali MulunguMwiniwake. Ena awiriwo anali Angelo a uthenga.

56 Tsopano,kumusi ku Sodomu, iwo sanachite zozizwitsa zili zonse, koma kungowapatsa iwokhungu. Ndipo kulalikira Uthenga nthawi zonse kwawakantha iwo ndi khungu.

Tsopanotayanganani chikhazilitso cha tsiku lija. Apo pali mpingo wachinthupi. Nthawizonse mu patatu, monga ine ndinenanso usiku watha, Mulungu amaimiriridwa. Apopanali Achisodomu; Achiloti ndi achiAbrahamu. Izo zili m'malo ofanana usiku uno, dziko lilinkukhala basimonga choncho.

Ndiloreniine ndikufunseni inu chinachake. Taonani momwe izi ziliri pano. Abrahamuamutcha Mamuna uyu yemwe amayakhula kwa iye, "Elohim." Liwu la chi Heberi Elohim limatanthauza"Okhala ndi chilichonseyo, Iye amene ali wa Muyaya," Elohim, Mulungu Mwiniwake!

Pachiyambi,Genesesi 1, anati, "Pachiyambi Mulungu . . ." Tenga liwu la chi Heberi pamenepo, mwina, kapena liwu la chigriki, kani,"Pachiyambi Elohim analenga Kumwamba ndi dziko lapansi."

57 Pano,Iye, mu Genesesi, pafupi 22 pano, Iye akulankhulanso, kapena-kapena pa 20, Iyeakuti, ndipo iye anamutchula dzina la munthu uyu "Elohimu." Kodi ndi chifukwa chiyani iye anachitaizo? Mulungu, akuimiriridwa mu thupi lamunthu, amene anakhala pansi ndi Abrahamu nadya sangweji ya mwana wa ng'ombe,namwa mkaka, nadyanso mkate. Mulungu Mwiniwake, ndipo anasowa apo pamaso paabrahamu. Koma Iye anampatsa iye chizindikiro. Zindikirani. Ndipo chizindikiroicho chinali choti Iye anali atatembenukira mbuyo Yake ku hemayo. Ndipokumbukirani, Abrahamu, dzina lake anali Abram masiku anagapo asanafike apo,ndipo Sarra anali Sarai asanafike apo; S-a-r-a-i kenako S-a-r-a-h ndipoA-b-r-a-m kukhala A-b-r-a-h-a-m. Abrahamu amatanthauza "atate wa mafuko."

Tsopanopenyani mwatcheru apa, ndipo ife tiona chikhazikitso cha ora lomwe ife tikukhalamo, monga Yesuanatiuza ife kuti tiyembekezere chikhazikitso ichi. Ife taona izo zonse za izomolondola; tsopano tiyeni tione ku Mbewu yachifumu, kuti ndi chikhazikitsochanji chomwe iwo ayenera kuti achione.

TsopanoMamuna uyu anati, "Abrahamu, ali kuti mkazi wako, Sarah?"

NdipoAbrahamu anati, "iye ali mu hema kumbuyo kwanuko.

Tsopano,Iye anali asanamuone iye (mkaziyo) Kodi Iye anadziwa bwanji dzina lake anali Abrahamu? Kodi Iye anadziwa bwanji kuti dzina anali S-a-r-a-h? "Abrahamu, ali kuti mkaziwako, Sarah?"

Anati,"Iye ali mu hema kumbuyo Kwanu."

Iyeanati, "Ine . . ." "Ine," Mulowa mmalo wa dzina wa umwini "Inendidzakuchezerani inu monga mwa lonjezo. Mkazi wako akhala naye mwana ameneyo.Iwe wandikhulupirira ine, tsopano Ine ndikufuna kuzipanga izo kuti zichitike.

58 NdipoSarah, muchihema, kumbuyo, akumvetsera mwakachetechete zokambirana za mserikapena ("eardropping,") muli monse momwe inu mumatchulira, kumamvetserakupyolera mu hema, iye anatseka monong'ona, ndipo iye anati, "tsopano, ine mayiwokalamba ngati ine, kukhala ndi zosangalatsa ndi mbuye wanga; ndipo nayenso,okalamba, kunja uko wa zaka zana zakubadwa? Pamene izi sizinachitike kwa zakazambirimbiri."

NdipoMwamunayo, M-W-A-M-U-N-A-Y-O atakhala apo akudya ali mu thupi la munthu, akumwandi kudya ngati munthu wamba, ali ndi fumbi pa zovala Zake, ndipo anali ndifumbi ku mapazi Ake, ndipo Abrahamu anamusambitsa Iye. Mulungu, Mwiniwake,anayang'ana pozungulira ndipo Iye anati, "chifukwa chiyani Sarah anaseka,kumbuyo mu hema, nati ichi?" Iye anadziwa, amakhoza kudziwa malingaliro a Sarahmu hema kumbuyo Kwake. Uko nkulondora? (Osonkhana anena, "Ameni."-Mkonzi.)

Tsopano,pamene mbewu yachifumu ya Abrahamu inabwera pa dziko lapansi, chizindikirochanji chomwe lye anaonetsa, Mwana wa munthu. Simon anabwera kwa Iye tsikulina; Andrea anamubweretsa iye. Iye anati, "Dzina lako ndiwe Simon. Iwe ndiwemwana wa a Yonasi," Iye anati. Mwaona, icho

chinamupanga kukhala okhulupirira.

59 Filipoanapita nakaitana Natanaeli; bwerera anati, "Bwera uone Munthu Yemwe ifeta-tamupeza; Yesu wa ku Nazareti, mwana wa Yosefe."

Iyeanati, "tsopano tadikira mpindi. Kodi pakanakhala chinthu chabwino chotulukamwa wotengeka uja?"

Iyeanati, "Bwera, uone."

Kotero pameneFilipo anabwera pamene Yesu anali, ndi Natanaeli, Yesu anayang'ana pa iye ndipoanati, "Taonani Mu Israeli yemwe mwa iye mulibe ndulu."

Iyeanati, "Rabbi, kodi Inu munandidziwa ine liti?"

Anati,"Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansi pa mtengo Ine ndinakuona iwe."

Iyeanati, "Rabbi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu. Inu ndinu Mfumu ya Israeli!"

60 Pamenemzimayi wamng'ono pa chitsime, mu chikhalidwe chake chachigololo, anabwerapo,mooneka bwino motero pang'ono chinachake monga chonchi, kuti akatunge madzi.Yesu anali atatumiza ophunzira Ake kutali, kuti akagule zokudya. Pamene iyeanabwera kudzatunga madzi, Iye anati, "Ndipatse Ine akumwa, mkazi."

Iyeanati, "Sikoleledwa mwa mwambo kuti Inu munene chimenecho. Ife tili ndi tsankhokuno. Tsopano, muAyuda mulibe chilichonse chochita ndi ife a Samaria; ifetilibe chochita ndi inu."

Iyeanati, "Koma, mkazi, ngati iwe ukanadziwa Yemwe iwe ukulankhula naye,ukanandifunsa Ine akumwa. Ine ndikanakupatsa iwe madzi omwe sungabwere kunokudzatunga."

Iyeanapeza pomwe panali chikhalidwe chake,chomwe icho chinali. Iye anati, "Pita ukatenge mamuna wako ndipo ubwere kuno."

Iyeanati, "Ine ndilibe mamuna aliyense."

Iyeanati, "Iwe wanena choonadi. Iwe wakhala uli nawo asanu, ndipo amene ukukhalanaye pano siwako."

Iyeanati, "Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi inu Mneneri. Ife tikudziwa kutipamene Mesiya abwera Iye adzationesa ife zinthu izi."

Yesuanati, "Ndi Ine amene."

Paicho, Iye anathamangira mu mzinda ndipo anati, "Bwerani, muone Munthu Yemwewandiuza ine zinthu zomwe ndinachita. Kodi uyu Si Mesiyayo?"

61 Penyani,Iye anachita izo pa maso pa a Yuda, ndi a Samaria, koma osati kwa a mitundu. Amitundu, anthu ife, tinali achikunja m'masiku amenewo, mafuko enawo, kutengachibonga kumbuyo kwathu, kumapembedza mafano. Ife sitimayembekezera Mesiya aliyense. Koma amaonekera kokha kwa iwo amene akumuyembekezera Iye, ndipo ifetiyenera kukhala oti tidzimuyembekezera Iye. Koma iwo amene amadzinenera kutiamamuyembekezera Iye, mpingo iwo mwini, pamene iwo anaona icho chikuchitika,iwo anati, "Uyu ndi mdierekezi. Iye ali wa mbwembwe, Belezebule!"

NdipoYesu anati, "Tchimo limenero likanadzakhululukidwa kwa iwo," chifukwa Iye analiasanafe apobe. "Koma ," anati, tsiku lina Mzimu Woyera udzabwera ndikuchitachinthu chomwecho, ndipo kuyankhula liwu limodzi motsutsana ndi Iwo izosizizakhululukiridwa." Ilo ndi lero, pomwe Mawu onse ayenera kumangirizikapamodzi. "Kuyankhula liwu lotsutsana ndi Iwo; sizidzakhululukidwa mu dziko ilikapena dziko likubweralo."

62 Iyoinali Mbewu yachifumu ya Abrahamu. Ndipo pano Mbewu iyo yachifumu ya Abrahamuimene inabwera chifukwa cha chizindikiro icho cha Munthu ameneyo atakhalapamenepo ndi Abrahamu, anabwera kudzatsimikizira kuti anali Mulungu yemweolonjezedwa ku tsiku ili, "Monga zinaliri M'masiku a Sodomu, momwensozidzakhala pa kubwera kwa Mwana wa munthu, pamene iwo akudziulula yekha ngatiMwana wa munthu." Ameni. Ili ndi tsiku loti Lemba ili likwaniritsidwe.

Penyanimomwe zinthu zakhalira uko lero. Penyani mpingo komwe Mwana wa Mulungu . . .Penyani pa tsiku lolunda. Penyani pa mauneneri onse. Tsopano, chinthuchachilendo, alendo athu ali pafupi ndiyeno, ngati chikhalidwe chiti chikhalengati ku Sodomu.

Apopanali atatu a iwo omwe anabwera apo, amuna atatu odabwitsa ochokera Kumwamba.Ife tivomereza zimenezo. Atatu a iwo; Mmodzi anatsala ndi Abrahamu. Iwo onseanayambira kumeneko, koma M'modzi anatsala ndi Abrahamu. Ena otsalawo anapitakumunsi mu Sodomu. Nkulondola uko?

(Osankhanaanena, "Ameni."-Mkonzi.) Ndipo Abrahamuanasinthidwa dzina, kuchoka kwa Abramu kukhala Abrahamu. Nzoona? ("Ameni.") Sipanakhalepo nthawi mu mbiri,mpingo wa dziko, anakhalapo ndi Mlaliki kupita ku iwo, ali ndi dzina lothera muh-a-m, kufika lero, Billy G-r-a-h-a-m.uko nkulondola? (Osonkhana anena,"Ameni."-Mkonzi.) G-r-a-h-a-m, zilembozisanu ndi chimodzi. A-b-r-a-h-a-m ndi zilembo zisanu ndi ziwiri. Koma G-r-a-h-a-m ndi zilembo zisanu ndi chimodzi,chomwe ndi dziko, munthu. Mwaona?

63 Tapenyanichomwe chinatuluka kumeneko, Lero, ndi azitumiki awo ochokera Kumwamba. Kodipali munthu pa dziko lapansi amene walalikira kulapa momveka bwino ngati BillyGraham? Kodi pakhala pali munthu yemweanali ndi kukhuza pa anthu, ngati Billy Graaham? Apo sipanakhale, munthu pa dziko lonse. O,Billy Sunday, ndi ena otero, anali muno mu United States, koma Billy Grahamamadziwidwa dziko lonse. Mukuona komwe iye akuitana? Kuchokera ku Sodomu. Ndipoiye ali naye mzake pamodzi naye uko ndi mpingo wa chi Petekoste, Oral Roberts.

Komakodi bwanji nanga gulu la Osankhidwalo. Kodi ndi chizindikiro chanji chomwe iwoayenera kuti achione? Kodi iwo akuyenerakukhala ndi chiyani? Alleluya! "Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya madzulo." Lero Lemba ili lakwaniritsidwa. (Osonkhana asangalala-Mkonzi.) Lero Lonjezo la Mulungu lakwaniritsidwa. Ifetikudziwa icho kukhala Choonadi. Iye ali pano usiku uno monga amene analirikumbuyoko.

64 Tsopano,kuchilalikira icho, zomwe ine ndinanena kanthawi kapitako, ngati iweungalalikire chinthu chirichonse ndipo icho nachikhala Uthenga wa Choonadi,pamenepo Mulungu ndi okakamizika kukatsimikizira icho. Uko nkulondola? (Osokhanaanena, " Ameni."-Mkonzi.) Tsopano ngatiizoziri choncho, Lolani Mulungu yemwe analemba Mawu, Muloreni Mulungu yemweanapanga uneneri, Lolani Mulungu yemwe ali Mulungu wa Mawuwo, abwerenatsimikizira kuti Iye adakali Mulungu.

MongaEliya anapita pamwamba pa Phiri; akupenyerera, Elisha anapita akupenyereraEliya, iye anati, "Ine ndikufuna magawo awiri." Ndipo chofunda chomwe chinali pa Eliya chinagwera pa Elisa. Iye anayendakutsikira kumunsi, napinda chofundacho kawiri ndipo anakantha mtsinjewo, ndipoanati, "Ali kuti Mulungu wa Eliya?" Ndipo chinthu chomwecho chomwe chinamuchitikiraEliya, chinamuchitikira Elisa. Ndipo Uthenga omweo, Mphamvu yomweyo, Mwana wamunthu yemweyo yemwe anali dzuro, ali lero ndipo adzakhala kwa nthawi zonse.Aheberi 13:8. Kodi inu mukukhulupirira icho?

(Osonkhana anena"Ameni."-Mkonzi.) Ndiyeno, Inendikukufusani inu. Ine sindingakhale Iye, koma Iye ali pano. ("Ameni.") Ife ndife kokha chotengera.

65 Enaa inu anthu kunja uko, amene muli odwala ndi osautsika, omwe mukudziwa kuti inesindikukudziwani inu, muloreni Mulungu tsopano . . . Ngati ine ndingathekudzichepetsa ndekha mokwanira. Inu mupemphere ndikumufunsa Mulungu.

Inesindimapenekera . . . Apa palibe kadi ya pemphero m'nyumba ino, kodi liripo?Ai, Ine sindi . . . Ife sitinaperekeKadi iliyonse ya mapemphero. Ife tikhala ndi msonkhano wa pemphero ku ...Kapena wa machiritso a odwala, ku kachisi. Koma, inu pempherani. Ndipo inumukudziwa kuti ine ndine mlendo wathuthu kwa inu. Mwaona, inu mukundidziwa ine,Jeffersonville! Ine sindikufuna anthu ochokera ku Jeffersonville kuti achiteizo. Ine ndikufuna ochokera kutaliochokera kuno kwinakwake. Mwaona ngati Mulungu akuululabe! Mwaona ngati Iyeadakali yemweyo dzuro, lero ndi ku nthawi zonse!

Chitanimonga anachitisa mkazi wamng'ono uja. Iye anadutsa pakati, ndipo iye anati,"Ine ndikukhulupirira munthu uyu." Iye anali ndi nthenda ya magazi, ndipoanati, "Ngati ine nditangokhuza mphonje yachovala chake, ndikhulupirira kutiine ndichiritsidwa." Nkulondola uko? Chifukwa cha chikhulupiriro chake, tsikulimenelo Lemba linakwaniritsidwa. "Iye anamangiriza mtima wa osweka mtima,anachiza odwala ndi opunduka."

Pameneiye anakhuza chovala chake, nayenda kupita kunja ndikukhala pansi, Iyeanatembenuka nati, "Ndani wandikhuza Ine?"

Kodi Iye akanadziwabwanji, mu unyinji waukulu wa anthu uja, pafupifupi kuchulukitsa makumiatatu kwa umo tiriri pano usiku uno,zikwi za iwo? Kodi Iye anadziwa bwanji? Iye anati, "Ndani wandikhudza Ine?" Iyesananene izo mongonena basi ai; Iye anena izo chifukwa icho chinali Choonadi.Ndipo Iye anati, "Ndani wandikhuza Ine?" Ndipo molunjika anayang'ana pozungulira ndipo anaona mkazi wam'ng'onoyo,pomwe anakhala kapena kuimirira, muli monse momwe iye analiri, namuuza iye kutivuto lake la magazi linatha. Uyo anali Yesu dzulo. Uyo ndi Iye lero.

Kodi inu mukukhulupirira izo? (Osonkhana anena,"Ameni."-Mkonzi.)

66 Inesindikukudziwani inu; Mulungu anakukudziwani. Koma inu muli ndi ululu pa mbalipanu omwe wakhala ukukusowetsani inu mtendere. Uko nkulondola. Inu mwakhala apomukupempherera icho. Kodi ine ndine mlendo kwa inu ndipo ndife alendo kwa winandi mzake? Imirira, ngati ndi choncho. Ine sindikukudziwani inu. Ndi mamuna uyupano cha pa ngodya, mamuna wachinyamata uyu. Inu mulinso nkukhosi koipa. Ukonkulondola. Inu munapempherera za icho. Inu ndi wamanjenje za chinachake. Inu muyenera kuchoka mu msonkhano chifukwa,inu ndi mtumiki, inu muli ndi ntchito zina zomwe muyenera

kuti mukachite. Uko mkulondola. Uh-huh. Inumukukhulipirira kuti Mulungu akudziwa kuti ndinu ndani? M'busa, Bambo Smith,tsopanopitani ndipo namuchiritsidwa. Yesu Khritu wakuchiritsani inu. Pitani kumsonkhano wanu; kukhosi kwanu sikungati kukuvuteniso inu. Kodi m'bamboyuwakhuza ndani?

67 Palimamuna yemwe wakhala cha kumbuyo kuno; Iye akuvutika. Iye ali ndi chotupa pamapapu ake a ku manzere. Iye sama . . . Iye si ochokera kuno. Inu mwakhalamukugwirira ntchito mu mgodi. Uko nkulondola. Ine ndine mlendo wathunthu kwainu. Ngati uko mkulondola gwedezani dzanja lanu. Chotupacho chili mu mapapu anua kumazere, ndipo inu mukupita kukapangidwa oparashoni pompopompo. Nkulondolauko? Inu si wa kuno. Inu ndi inu wa kunja kwa tauni. Inu mumachokera kuVirginia. Uko nkulondola. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akudziwa chomweinu muli? Bambo Mitchell, uko nkulondola, pitani kwanu ndipo mukhala bwino.Yesu Khristu wakuchiritsani inu mufunsani bamboyo! Sindinamuonepo m'moyo wanga.Iye anakhala apo akupemphera. Lero Lemba ili!

(M'bale Branham atembenuzira msana wake kwaosonkhana-Mkonzi.) Apa pali dona yemwe wakhala cha ku mbuyo kuno, kumbuyikwanga monga Sarah anali mu hema. Iye akupempherera mwana wake wa mkazi.Imirira. Mwana wa mkaziyo sali pano; iye ali kutali mwana wa mkaziyo. Ndipo inumuli chimodzimodzi monga zinaliri pamene mkazi anabwera kwa Yesu, yemwe analindi mkazi yemwe anali atasautsidwa mochuluka ndi mdierekezi. Mkaziyo ndi . . .Mtsikanayo wagwidwa ndi ziwanda. Iye sali pano. Iye amachokera . . . inumumachokera ku North Carolina. Inu mukukhulupirira zimenezo? Ndipo icho ndichoonadi, si choncho? Mai Orders, inu mutha kupita ku nyumba. Ngati inumungakhulupirire ndi mtima wanu onse, inu mukamupeza mwana wanu wamkazi mongaanampezera pamene Yesu Khristu mu masiku apitawo, ananena kuti anachiritsidwa.

68 LeroLemba ili; chizindikiro cha ku Sodomu, chizindikiro cha Mbewu yopambana,chizindikiro cha mpingo wa chithupi! Lero Lemba ili lakwaniritsidwa pakatipanu. Kodi inu mukukhulupirira ichi? (Osonkhana anena, "Ameni."-Mkonzi.) Kodiinu mungamulandire Iye pakali pano ngati Mpulumutsi wanu, Mchiritsi? Imiriranipa mapazi anu, aliyense wa inu, nenani, "Ine ndikulandira machiritso anga.Ine ndikumulandira Iye ngati Mpulumutsiwanga. Ine ndikumulandira Iye ngati Mfumu yanga." Aliyense wa inu imirirani pa mapazi anu.

Lero!Mvetserani, abwenzi. "Iye anawerengaLemba, nabwezera kwa wamsembe, ndipo," anati "maso onse a anthu analiatamangirizidwa pa Iye. Ndipo Iye anayang'ana pa iwo, ndipo anati," LeroLemba ili lakwaniritsidwa.

Inendawerenga Lemba, ndi umboni khumi ndi uwiri kapena ochulukirapo kuti ifetikukhala mu tsiku lotsiriza, M'badwo omwe uti udzaone Yesu Khristu akubwera kudziko. Ndipo ine ndikunena kwa inu usiku uno, kachiwiri, Lero Lemba ililakwaniritsidwa nkupenya kwanu.

Inuku Tucson, inu ku California, inu ku New York, mu kulumikiza kwa lamya uku,Lero Lemba ili lakwaniritsidwa nkupenya kwanu. Tiyeni ife tisangalale ndikukondwera, pakuti chikwati cha mwanawankhosa chayandikira, ndipo mkazi wake .. . Mkazi Wake wazikonzekeretsa yekha.

Tiyenitonse tikweze manja athu ndikupatsa Iye Ulemerero, inu anthu nonse. Mulunguakudalitseni inu. (Osonkhana apitiriza kusangalala ndi kutamandaMulungu-Mkonzi.)

MESSAGE online

www.messagehub.info

Maulaliki wolalikidawa ndi

William Marrion Branham

"...mu masiku a liwu..." Chivumbulutso 10:7